Mafunso ndi Mayankho

Ndipo ine ndiri wokondwa kukhala ndiri muno kachiwiri usikuuno mu utumiki kwa Ambuye wathu. Ndipo tsopano, pokuonani inu nonse okondwa ndipo mukuimba nyimbo zodabwitsa zakale izi, onse mutadzazidwa ndi mzimu ndi zina zotero, zikutipangitsa ife kumverera bwino kwenikweni.

2 Ndipo ife tiri okondwa kuti tiyesere kutenga mphindi pang'ono za nthawi kachiwiri usikuuno kuti tiyankhe funso kapena awiri. Ife tinakhala ngati ndinatenga nthawi yanu yochuluka mmawa uno, koma ine ndikuyembekeza inu munalandira dalitso lomwe ine ndinalandira pakungoyankhula za izo. Ndi . . . Inu mukudziwa, ife tiri ndi zambiri zoti tizizikamba, sitiri ife? Ndipo ife tiri naye Munthu woti tizimukamba, ndiye Ambuye wathu Yesu.

3 M'bale Teddy, ngati ine ndikanati—ngati inu mungalole, inu mungotsalira pomwe pano mphindi yokha. Ine ndinauzidwa kuti panali mwana wamng'ono wodwala mu nyumba ino.

4 Ndipo ine ndisanayambe pa izi, ife tiri ndi Mgonero, chotero ife tikufuna—sitikufuna kuti titenge nthawi yochuluka kwambiri—ndipo mwinanso ubatizo. Ndipo chotero ine—ine ndikufuna ku—kuti ndiwapempherere awo amene akufuna kuti apemphereredwewo choyamba, kuti ichi, kuti tiwapempherera odwala choyamba, ine ndisanati ndiyambe.

5 Ndipo tsopano, ngati . . . Teddy, ngati inu mungati, muziyimba nyimbo iyi, *Sing'anga Wamkulu Tsopano Ali Pafupi*. Ndipo ife tikuti tiwaitane odwala ndi kupemphera madalitso pa iwo pano. Ndi angati ali pano ali oti apemphereredwe usikuuno? Panali ena omwe ife tinawaphonya mmawa uno. Kodi mungakweze manja Ngati inu mungawakwezetse manja awo mmwamba, ngati inu . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . ndi kumva umboni umenewo, ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha ubwino Wake wonse. Mulungu alemekezeke kwa yemwe madalitso onse amayenderera. Ndi kulondola uko?

6 Tsopano, ife tikhala tikuyamba mwamsanga momwe pa maumboni awa tsopano, ndipo ife tikuti tiyesere, kapena, ndikhululukireni ine, pa mafunso. Ndipo ine ndikuyembekeza kuti Mulungu angokhuthulira madalitso Ake mmenemo m—mwa njira iyi.

7 Ndipo tsopano, musati mundirole ine ndipite motalikitsa kwambiri pa iwo. M'bale Cox, ine ndikuti ndiitanitse tcheru chanu, inu ndi madikoni amene akhala pa mzere wapatsogolopa, kuti mundiimitse ine pamene ine—pamene iyo ifika moyandikira nthawi yoti mutipatse ife Mgonero (inu mukuona?), chifukwa

ine ndimawasunga iwo motalikitsa kwambiri. Ine ndiyesa kupita mofulumira basi momwe ine ndingathere. Ndiyeno, ngati ine sindiwatsiriza iwo Lamlungu ili, ine ndidzawatenga iwo Lamlungu lotsatiralo; ayi, ine ndiyesetsa kuti nditsirize usikuuno.

8 Iwo ndi mafunso abwino chotero. Ndipo ine ndikukuuzani inu, abwenzi, ngati chikanati chisakhale chitsitsimutso ichi ndi zinthu zikuchitika, ine ndikadakonda ndikanakhala pafupi sabata pa kuphunzitsa kokha kolunjika kwa pa Baibulo p—pa Genesis, ndi Eksodo, ndi Chivumbulutso, ndi ena otero, n—ndi kungokhala ndi n—nthawi yabwino kwenikweni. Ine ndimawakonda mafunso akuya a Baibulo ndi kuphunzitsa kwa Baibulo, bola ngati inu simupita ku chinthu chinachake chopeka. Kungokhala molunjika basi momveka, Mawu a Mulungu osasokonezedwa, achikale; Iwo akudutsitsani inu molunjika kumene. Inu simukukhulupirira izo?

9 Chabwino kuti, mmawa uno, ife tinali nawo e—ena a mafunso abwino zedi, ena a iwo okhudza handiredi ndi forte-foro sauzande, iwo anali ndani, ndi gawo lomwe iwo ati adzakhale ali? N—ndi zokhudza Mkwatibwi. Ndipo o, zinthu zambiri basi, ndi basi mafunso ozama kwenikweni. Ndipo ine ndinali nao angapo omwe ine sindinafike powamaliza.

10 Tsopano, usikuuno ife tikuti tiyambire apa pomwe pa limodzi ili, ndipo tiwafunse Ambuye kuti atithandize ife. Ndipo tsopano, ife sitingakhoze kulitsegula Baibulo. Ife tikhoza kulitsegulira Ilo monga chonchi, koma zimatengera Mulungu kuti alitsegule Ilo kwenikweni kwa ife. Ife tikhoza kukoka masamba. Koma mu Bukhu la Chivumbulutso, pamene Yohane anayang'ana, ndipo iye anaona Mmodzi atakhala pa Mpandowachifumu, ndipo apo panali—Iye anali ndi Bukhu mu dzanja Lake. Ndipo apo panalibe munthu yemwe anali woyenera kuti alitenge Bukhulo, kapena kuti amatule Zisindikizo, kapena ngakhale kuti ayang'ane pa ilo. Kunalibe munthu Kumwamba, kunalibe munthu pa dziko lapansi, kapena kunalibe munthu pansi pa dziko, kapena popanda kulikonse anali—anali woyenera. Ndipo iye anamuona Mwanawankhosa, wonga ngati Iye anali ataphedwa kuchokera ku maziko a dziko. Ndipo Iye anadza ndipo anadzalitenga Bukhulo kuchokera mdzanja Lake ndi kutsegula Zisindikizo; Uyo anali Yesu Khristu.

11 Tsopano, ine ndinali kuyankhula kwa munthu Sabata ino, mwamuna wazamalonda wochitabwino kwambiri mu mzindawu, yemwe ananena kwa ine za kubwereranso ku Afrika ndi India: iye anati, "Bwanji, iwo angomupha kumene mkulu wankhondo wa Chibritishi kumeneko."

Ine ndinati, "Izo ziri ndi chochita chanji ndi ine?"

Iye anati, "Inu mubwerera uko kumene kuphana konse kukuchitika, kuukirana mitundu uko, ndi zina zotero?"

Ine ndinati, "Zedi, ndi kumene ine ndikufunika, kumene Ambuye akufuna kuti ine ndipiteko."

Iye anati, "Nanga bwanji ngati iwo ati akakuphe iwe?"

Ine ndinati, "Chabwino, ngati Mulungu akufuna kuti ine ndiphedwe, ine ndikangophedwa basi, ndizo zonse."

Ndipo iye anati, "O, mai!" Anati, "M'bale Branham, inu simuyenera kumaganiza choncho. Chabwino," anati, "Ine sindikusamala. Ine ndikuganiza ndinu wachipembedzo, ndipo ine ndikuganiza ndinu munthu wabwino," iye anati "koma iwo anamupha ngakhale Yesu Khristu."

Ine ndinati, "Zedi, icho chinali chifuniro cha Mulungu."

Iye anati, "Chiani? Chifuniro cha Mulungu?" Ine. . . Ndipo bambo ameneyo wakhala akupita ku mpingo (ali moyandikira ku sevente)—wakhala akupita ku mpingo. . . Iye anali mu kaundula wakuubwana wa mpingo wabwino wa mu mzinda muno, ndipo wafika mpaka—ndipo samadziwa nkomwe kuti icho chinali chifuniro cha Mulungu kuti Yesu afe.

12 Chifukwa, ine ndinati, "M'bale, Iye anaphedwa kuchokera ku maziko a dziko, kuchokera ku chiyambi komwe. Iye anaphedwa Iye asanabwere nkomwe ku dziko lapansi." Nkulondola uko? Iye anali Mwanawankhosa wa Mulungu wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi.

13 Tiyeni ife tiyankhule kwa Iye kamphindi kokha chifukwa cha mafunso awa. Tsopano, Atate, ife sitiri oyenera, ndipo sitiri okhoza, ife tikuzindikira, kuti titsegule Bukhu kapena kuyang'ana pa ilo. Koma muloleni Mwanawankhosa abwere tsopano usikuuno, Mwanawankhosa wa Mulungu amene anaphedwa kuchokera ku maziko a dziko, atenge zinthu zimene ziri za Mulungu ndi kuzipereka izo kwa osonkhana awa. Mulole Mzimu Woyera uwanyamule mawu awa, ndipo asati akhale mawu anga kapena mawu a munthu, koma mulole iwo akhale Mawu a Mulungu kwa mtima wanjala uliwonse. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

Loyamba lake pano (ife sitinawaike iwo mudongosolo kapena chirichonse, koma basi momwe iwo akudzera), iwo akuwoneka kuti ndi abwino kwambiri. Choyamba, ndi angati amene ali kukondweretsedwa nawo mafunsowa, tiyeni tione anu. . .? Chabwino, izo nzabwino kwambiri. Momwe ine ndikudziwira.

15. Tsopano. **Kodi munthu pa imfa amapita Kumwamba kapena—pena ku hade pomwepo, kapena kodi iwo amayembekezera chiweruzo?**

14 Ilo ndi funso labwino kwambiri. Ndipo likuchita—linali loyenera kulilingalira bwino mochuluka, chifukwa munthu aliyense ndi wokondweretsedwa, chomwe iye ati adzakhale moyo uno ukadzakhala utatha? Munthu aliyense ndi

wokondweretsedwa. Chabwino tsopano, ine—kwa gawo langa, i—ine sindikanati ndidziwe. Ine ndikuyenera kuti ndiyankhe kuchokera mu Baibulo.

15 Ine ndikulingalira mkazi wina anapanga foni yokwanira madola fifite kanthawi kapitako kuchokera ku Los Angeles, pafupi maminiti sate-faifi kapena forte, kapena mwina motalikirapo, ku malo akutali, kuyesera kuti andipeze ine kuti ndinene kuti izo zinali zovomerezeka ndi zolondola kuti iye amusiye mwamuna wake ndi kukwatiwa ndi mwamuna wina. Ine sindikanachita izo. Ayi! Ine ndinati, "Ayi, bwana!"

Iye anati, "Chabwino, mwamuna wanga ndi wochimwa, ndipo mwamuna uyu ndi Mkhristu."

16 Ine ndinati, "Izo ziribe kanthu kochita ndi icho. Inu mukhala muli mu chigololo motsimikiza monga chirichonse."

Anati, "Chabwino, ine ndine wachifuwa chachikulu, ndipo palibe chifukwa chirichonse kwa ine choti ndikhalire moyo ngati ine sindingakhoze kukhala naye mwamuna uyu."

17 Ine ndinati, "Inu mwangotengeka ndipo osati mu chikondi, chifukwa inu simukanakhala muli, ndizo zonse, chifukwa uyo ndi mwamuna wanu. Ndipo ndinu olumbirira kuti muzikhala ndi iyeyo mpaka imfa idzakulekanitseni inu. China chirichonse chochotsera apo, iwe uli mu chigololo." Ndipo chotero, iye anangopitirira kugwirabe. Ine ndinati, "Dona, palibe kufunikira . . . "

Iye anati, "Ngati inu muti mungondiuza ine kuti izo zonse nzabwino."

Ine ndinati, "Ine sindingachite izo." Ine ndinati, "Ine ndi . . . "

Iye anati, "Chabwino, M'bale Branham, ife tiri ndi chidaliro chochuluka kwambiri mwa inu."

18 Ine ndinati, "Ndiye mvetserani ku chimene ine ndikuyesera kukuuzani inu. Ine ndikukuuzani inu Choonadi, pakuti ine sindingakhoze kunena kanthu kupatula chimene Mulungu ananena." Mulungu anati izo nzoona, kotero izo ziri ndendende basi momwe izo ziriri. Mwaona? Ine ndinati, "Umo mmomwe i—izo zikuyenera kuti zizikhala ziri, ndipo umo ndi momwe izo ziyenera kukhalira ziri."

19 Ndipo tsopano, mu mafunso awa, ndi momwe ife tikuwafunira iwo kuti akhale ali. Tsopano, izo nthawizonse zimaganiziridwa . . . Tsopano, mkati muno, inu mukuzindikira, mwa anthu apang'ono ammanja awa usikuuno, muli mwinamwake mitundu yonse ya malingaliro osiyana; ndipo ife tikuganiza kuti iwo onse ndi abwino, limodzi lirilonse la iwo. Ganizo lanu ndi labwino, ndipo liri . . . Koma tsopano, chimene titi tichite, ife tiyenera kukhala naye winawake . . . Monga momwe atsekwe, abakha, chirichonse, chirichonse chiyenera—

njuchi—zirizonse ziri naye mtsogoleri. Ngati mfumukazi wa njuchi afa, inu mukudziwa chimene chimachitika. Bakha wotsogolera akafa, iwo amayenera kudzipezera mmodzi wina. Kuti, iwo amangoyenera kuti akhale naye mtsogoleri.

20 Ndipo munthu ayenera kuti azikhala ndi mtsogoleri; ndipo mtsogoleriyo ndi Mzimu Woyera. Ndipo Mzimu Woyera unakhazikitsa mu Mpingo poyamba, atumwi, pambuyo pake, aneneri, ndi ena otero.

Winawake ananena osati kale kwambiri, anati, "Bwanji, M'bale Branham, ife sitikusowa winawake kuti azitiphunzitsa ife. Pamene Mzimu Woyera ubwera, ife sitimasowa aliyense kuti azitiphunzitsa." Anati, "Baibulo limati inu simusowa—simusowa kuphunzitsa."

21 Ine ndinati, "Ndiye nchifukwa chiani Mzimu Woyera womwewo unayika mu Mpingo aphunzitsi, mwaona, mwaona, ndipo anauyika Mpingo mu dongosolo?" Iwo akanadza . . . Ife tiyenera kumakhala nao aphunzitsi. Ndiko kulondola.

22 Koma inu simuyenera kuti muzikhala ndi winawake . . . Simukusowa kuti azikuphunzitsani inu kumati, "Inu musatimuzichita chigololo; inu musati muzilumbira, ndi kutenga . . . " Inu mukudziwa kale izo. Chikumbumtima chanu chomwe cha Mzimu Woyera chimakuuzani inu kuti nzolakwika kuti muzichita izo.

23 Koma tsopano monga mwa chiphunzitso cha Mwamalemba, izo zimatengera wodzozedwa ndi Mzimu Woyera. Ndiko kulondola. Ndipo Mulungu wauyika Mpingo mu dongosolo mwa atumwi ndi aneneri, ndi mphatso za machiritso, ndi zozizwitsa, ndi zina zotero. Iye wauyika Mpingo mu dongosolo ndipo waikamo aphunzitsi ndi ena otero mmenemo kuti aziutsogolera ndi kuulondolera Mpingo Wake. Ndipo mmawa uno, ife—monga ife tinanena, Yesu pamwamba pa dziko lapansi monga Thupi Lake . . . Ndipo monga momwe thupi Lake limasunthira, ziri basi monga mthunzi ukunyezimiritsidwa kwa dziko lapansi. Ilo lizisuntha limodzi nawo.

24 Tsopano, anthu ambiri . . . Anthu a Adventisti amakhulupirira kuti pamene munthu afa kuti iye amapita mu manda umo momwe ndipo amakakhala mmenemo, solo, thupi, ndi china chirichonse, mpaka pa chiukitsiro. Ndipo awo . . . Iwo amazitcha izo "kugona kwa solo." Chabwino, izo nzabwino. Izo nzabwino bola ngati iwo amamukhulupirira Yesu Khristu ndipo ali obadwa kachiwiri, izo siziti ziwapweteke iwo. Koma tsopano, molingana ndi Malemba, kuti pamene munthu afa, ngati iye ali Mkhristu, ngati iye ali wobadwa kachiwiri, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, iye sadzasowa konse kuti adzaime mu ziweruzo za Mulungu. Mwaona? Iye amapita molunjika mu kukhalapo kwa Mulungu. Ndipo iye sadzasowa kuti adzakhale mu chiweruzo, chifukwa iye ali kale . . . Mwaona?

25 Ine sindikusowa kuti ndiziimira pa chimene Khristu anandichitira ine. Tsopano, ine ndinali wochimwa, koma chiweruzo cha Khristu . . . Pano pali—pano pali chinthu champhumphu mwa mawu ochepa: Mulungu anati, "Tsiku limene iwe udzadya za iwo, tsiku limenelo iwe udzafa." Izo zinakhazikika.

26 Tsopano, Mulungu ayenera kuti azisunga Mawu Ake. Iye sangakhoze kuchita kanthu kalikonse kupatula kusunga Mawu Ake, chifukwa Iye ndi Mulungu. Chabwino ndiye, Iye sangakhoze. Ndiye, Iye . . . Inu ndinu olekanitsidwa kwa Mulungu . . . Ndiyeno, ndinu obadwa mu tchimo, owumbidwa mu kusaweruzika, kudza mu dziko nkumayankhula bodza. Chotero pamene inu mwabalidwa, ndinu ochimwa mwachibadwa. Chotero palibe chirichonse mu dziko chomwe inu mungakhoze kuchitapo pa icho. Palibe chirichonse ine ndingakhoze kuchita kuti ndidzipulumutse ndekha kapena inu kuti mudzipulumutse nokha. Ndi chimene Khristu anatichitira ife mwa Mulungu—kapena chimene Mulungu anatichitira ife mwa Khristu. Mwaona? Izo siziri, chabwino, ngati ine ndikuganiza *ichi* kapena ine ndikuchita *ichi*, izo ziri ngati Iye anazichita *icho*.

27 Chabwino tsopano, ife tiri mwa Iye. Ndiye Iye anaima ndi ziweruzo za Mulungu; Iye anatenga chiweruzocho. Ndipo Iye, pokhala wosalakwa kwa tchimo, wosadziwa tchimo ayi, komabe anapangidwa tchimo chifukwa cha ife. Chotero bola ngati iwe uli mwa Khristu, iwe ndiwe mfulu kwa chiweruzo. "Pamene Ine ndiwona Mwazi, ine ndidutsa pa inu." Mwaona, Mwaona? Ndi zimenezo. Mwazi, umene umatimasula ife.

28 Tsopano, wochimwa sama . . . Wochimwa adzayenera kuti adzaime pa chiweruzo. Ndipo sipadzakhala china koma chiweruzo ichi. Icho chiri ngati monga m—mkombero kapena utawaleza wozungulira dziko wa Magazi a Khristu. Bola ngati inu muli mkati umu . . . Ngati Mulungu angati ayang'ane pa dziko lapansi mu chikhalidwe chakechi usikuuno mwanjira ina iliyonse kupatula kupyolera mu Magazi a Khristu, Iye akanati aliwononge ilo mu kamphindi. Iye akanayenera kutero. Ndithudi Iye akanayenera kutero. Ndi pamene chiweruzo chiri kubwera.

29 Tsopano, ngati—kapena bola ngati munthu ali pansi apa, palibe kanthu kuti munthuyu ndi chidakhwa, ndi wanjuga, ndi wosakhulupirira woipa, zifundo za Mulungu zimamutetezera apobe iye. Ndipo mkazi, iye akhoza kukhala ali, chirichonse chomwe iye angakhoze kukhala ali, wachiwerewere kapena chirichonse, Magazi a Yesu Khristu amamutetezera apobe iye. Koma miniti yomwe moyo wake uchoka mthupi ili ndipo iye wapita kupitirira apo, iye wadutsa pa chifundo kupita ku chiweruzo. Mulungu wamuweruza kale iye. Izo zimakhazikitsa icho. Iye watheka. Iye waweruzidwa. Iye waweruzidwa.

30 Inu mumadziweruza nokha ndi momwe inu mumachitira nacho chitetezero cha Mulungu apo cha machimo anu. Mwaona? Inu mumadziweruza nokha. Inu simumuweruza Iye ngati wolungama kokwanira kuti akukhululukireni inu. Mwaona? Ngati inu mukuganiza kuti Iye akukhululukirani inu, vomerezani zolakwitsa zanu, ndipo Iye akukhululukirani inu.

31 Ndiye ndi Mzimu umodzi (zindikirani) ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi. Ndipo monga thupi ilo linaukitsidwa ndi Mulungu, kuukitsidwa kwa akufa, kulungamitsidwa, liri pa dzanja Lake lamanja mu mphamvu ndi ukulu Kumwamba, chomwechonso iwo amene ali okufa mwa Khristu, ali mwa Khristu, ndi omasulidwa ku chiweruzo, ndipo adzatulukirapo mu chiukitsiro.

32 Tsopano. Koma pamene ife tifa tsopano—pamene ife tifa tsopano, ife timapita molunjika mu kukhalapo kwa Mulungu Wamphamvuzonse mu thupi lakumwamba. Ngati ine ndikanakakomana ndi M'bale Neville kumwamba uko, ngati ife tonse titamwalira pano, mu ora kuchokera pano ine ndikanakomana naye iye; ine ndikanati, "Moni, M'bale Neville," kuyankhulana naye. Ine sindikanakhoza kumugwira iye chanza; iye ali mu thupi lakumwamba. Ine ndikanakhoza kuyankhula kwa iye; iye akanamawoneka basi momwe iye aliri apomo. Ine ndikanamawoneka momwe ine ndiririmu. Koma ife tikanakhoza kumayankhulizana wina ndi mzake, koma ife sitikanakhoza kumakhudzana wina ndi mzake, chifukwa ife tiribe iliyonse ya mphamvu zisanu za kuona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva. Mwaona? Koma ife tikanakhala tiri achisavundi, ndipo tikanamakhoza kumaonana wina ndi mzake. Ife tikanamakhala mu madela odala pambali pa guwa la Mulungu. Kodi inu simukudziwa kuti Yohane anayiona miyoyo pansi pa guwa ikulira, "Mpaka liti, Ambuye, mpaka liti" kuti abwerenso ku dziko lapansi kuti adzavekedwe pa iwo?

33 Ndiye, pamene Yesu, yemwe ali mwa ife tsopano mwa maonekedwe a Mzimu Woyera, pamene thupi Lake lakumwamba, Mzimu Woyera, adzabwerera ndi thupi laulemerero, ife tidzapatsidwa ulemerero limodzi Naye mofanana Naye. Mukuona chomwe ine ndikutanthauza? Ndiye ine ndizidzagwirana naye chanza nkuti, "Ndi uyu pano, M'bale Neville." Ndiye ife tidzakadya.

34 Penyani. Yesu anawauza ophunzira Ake, potenga Mgonero wao, Iye anati, "Ine sindidzadya kenanso za chipatso cha mpesa mpaka ine nditadzadya icho ndi kumwa icho limodzi nanu katsopano mu Ufumu wa Atate Anga." Ndi kulondola uko? Mwaona? Ndi zimenezotu. Chotero, ife . . . Pamene akufa amwalira . . . Munthu wolungamitsidwa, ataima mu kukhalapo kwa Mulungu, amapita mu kukhalapo Kwake monga munthu wosavunda ndipo amakhala mu madela odala a mtendere mpaka tsiku limene—adzabwereranso kuno.

35 Tsopano, inalipo nthawi yomwe anthu sankapita mu kukhalapo kwa Mulungu pamene iwo amwalira, olungamitsidwa. Izo zinali mu Chipangano Chakale. Iwo ankapita ku malo otchedwa Paradiso, ndipo kumeneko miyoyo ya olungama inkadikira mu Paradiso. Koma Paradiso anali malo kumene Mulungu ankasungiramo miyoyo mokhala ngati dziko la maloto, mpaka pamene Magazi a Yesu Khristu atakhetsedwa; pakuti magazi a ng'ombe ndi mbuzi sakanakhoza kulichotsa tchimo, iwo ankangoliphimba tchimolo. Koma Magazi a Yesu amachotseratu tchimo.

36 Inu muzindikira kuti Ake—pamene Iye anafa pa Gologota . . . Ndi pa kubwerera Kwake, Iye anawaturutsa kuchokera mmanda oyera okufa aja amene anafa pansi pa chitetezero cha magazi a ng'ombe, ndi mbuzi, ndi ana a ng'ombe. Ndipo iwo analowa mu mzinda (o!) ndipo anaonekera kwa ambiri. Kukongola kwake chithunzichi! O, ngati ife tikanakhoza kuchijambula icho mkamphindi chabe. Tayang'anani pa Yesu pamene Iye anafa.

37 Apa, monga ine ndimanena mowirikiza, ine ndikukhulupirira, mu mpingo uno, muli m—mndandanda pano monga, mkati umu mumakhala anthu achivundi. Ndipo aliyense ali mu chisokonezo chachikulu ichi cha kulakwa, cha kuda ndi mdima. Oti adzafa amakhala mkati umu. Tsopano, iwo ali mwina kukopedwa kuchokera ku njira *iyi*, kapena kuchokera ku njira *iyo*. Inu simungakhoze kukhala kuno chinthu chauzimu, wochimwa kapena woyera, popanda kukhala ndi kukopa kochokera ku dziko lapansi kapena kuchokera ku dziko lammwamba. Ngati inu mukukopedwa kuchokera kuno, ndinu ochokera mmwamba. Thupi lanu lakumwamba likuyembekezera mmwamba umu. Koma ngati inu muli wochimwa, ndi wachinyengo, ndi wosiyana, thupi lanu lakumwamba liri pansi apa, mosasamala mochuluka momwe iwe ukuganizira kuti ilo liri mmwamba umo; chifukwa chipatso chimene iwe ukubala pamaso pa anthu chikutsimikizira kumene iwe unachokera. Chotero inu muli pano chimene inu muli kwinakwakenso. Moyo wanu umene inu mumakhala kuno uli kungonyezimiritsa chimene cholandira chanu chiri pamene inu mudzachoka kuno. Kodi inu mukumvetsa?

38 Ife tiri pakali pano (o, pamene ine ndiganiza za izo)—ife tiri pakali pano kupatsidwa ulemerero mu kukhalapo kwa Mulungu, okhulupirira obadwa kachiwiri. "Pakuti ngati msasa wapansi uwu uti usungunuke, ife tiri nawo kale wina ukuyembekezera mu Ulemerero," osati kwinakwake, kutsidya komweko ukuyembekezera kale pano. Ndipo matupi a dziko lapansi awa akubuulira kuti avekedwe pa iwo chisavundi chimenecho. Nkulondola uko? Matenda, ndi zopweteka, ndi zowawa, ndi zokhumudwitsa, ndi kuwawamtima, ndi . . . O! Ine ndidzakhala wokondwa pamene chinyumba chatizilombo

chokalambachi chidzakhala chitatsekedwa, simudzatero inu? Inde, bwana! Ife tikhoza kupita Kwathu. Ndiko kulondola.

39 Kungoti, ife tiri...kubuula kuti tivekedwepo, Mzimu ukubuula. O, pamene inu muyang'ana ndi kuona kuwawa konse pozungulira pathu, chisokonezo chonsechi, kununkha, ndi tchimo, ndi kukhala moyo wachivundi, ndi chinyengo, ndi chirichonse, ine ndimaganiza, "O, Mulungu, ndi mpaka liti izi ziti zikhale ziri?"

40 Limodzi la masiku awa ine ndidzalalikira ulaliki wanga wotsiriza, ndidzaliika Baibulo pansi monga chonchi, ndi kupita Kwathu. O, nthawi yake yomwe iyo iti idzakhale ili. Ndipo pamene msasa wapadziko lapansi uwu watha kuno, iyo siidzakhala mphindi imodzi mpaka ine ndidzakhala ndiri mu lina ilo kutsidyako; momwemonso mudzatero inu. O, mai! Palibe zodabwitsa iwo anati:

> Mwinjiro uwu wa mnofu ine ndidzaugwetsa ndi kukwera,
>
> Ndi kutenga mphotho yosathayo;
>
> Ndi kumafuula ndikudutsa mu mlengalenga ...(Zedi,kusunthirabe mmwamba.)

41 Tsopano, uko ndi kuti? Ndi liti pamene ife tidzakhale nalo ilo? Pompano! "Iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsanso ulemerero." Ndipo kodi inu mukuzindikira kuti thupi lathu lachisavundi, laulemerero likudikirira mu kukhalapo kwa Yesu Khristu pakali pano, kutiyembekezera ife kuti tibwere?

42 Kodi inu mumadziwa kuti pamene khanda labalidwa mu dziko lapansi ili, ilo lisanabadwe liri nawo moyo. Koma ilo nkuti lisanabalidwe. Ndipo mwamsanga pamene khanda limenelo libwera po—iye—iye akayamba ku—akabalidwa... Mapapo ake onse ali otsekedwa, ndipo iye ndi wakufa. Akatumba ake amanjenjemera ndi kukoka. Koma chinthu choyamba, kukamenya kwakung'ono kokha kapena kuwiri monga choncho [M'bale Branham akuwonetsera—Mkonzi.], ndipo iko kamati [M'bale Branham akugwira—Mkonzi.] kamagwira mpweya wake. Chavuta nchiani? Mwamsanga pamene thupi lachibadwa ilo liri kupangidwa mwa mayiyo, pali thupi lauzimu likuyembekezera kuti limulandire uyo mwamsanga pamene khandalo libadwa.

43 Ndipo motsimikiza basi pamene thupi lauzimu ili liri kuumbidwa, pali thupi lachilengedwe limayembekeza kuti lililandire ilo mwamsanga pamene ilo limachoka mu dziko lino. Mwaona? Mosemphanitsa choncho, kubwerera basi ku Edeni kachiwiri (mwaona?), kungobwerera basi.

44 Tsopano mmenemo, Mulungu . . . Chifukwa imfa, izo basi—izo zimangoichotsapo mbola yonse ya imfa imene ilipo. Ndipo palibe zodabwitsa kuti Paulo akanakhoza kuima ndi kuti, "Imfa, ili kuti mbola yako? Manda, chiri kuti chigonjetso chako?" Iye anati, "Zikomo akhale kwa Mulungu yemwe amatipatsa ife chigonjetso kupyolera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu." Inde, bwana. Msasa uwu wa padziko lapansi ukasungunuka ife tiri nawo kale wina ukutiyembekezera, kotero ingoiwalani za ili.

45 Tsopano kwa inu, bwenzi, ngati inu muli wochimwa yemwe munafunsa izi, Mulungu akhale wachifundo kwa inu. Inde, bwana! Inu simuli kokha pansi pa chitsutso tsopano, osati kuno, ayi! Inu muzilemera ndi kumapitirira. Ndipo izo zonse ndi kupyolera mu zifundo za Mulungu. Izo zonse ndi kupyolera mu zifundo za Mulungu kuti inu muzilemera ndi kumachita zomwe inu mukuchita. Izo nzoona. Koma limodzi la masiku awa, ngati muli wochimwa ndipo moyo wanu ukachokamo, iwo udzapita kutali ku chiweruzo ndipo udzakaweruzidwa. Ndiyeno, inu mudzataidwa kutali, ndipo inu mudzakhala mu chizunzo mpaka tsiku limene inu muti mudzabweretsedwenso ku dziko lapansi ili kachiwiri. Ndipo inu mudzalandira thupi lachisavundi, thupi lachisavundi lomwe silingakhoze kufa, ndipo lidzaponyedwa uko ku mdima wakunja kumene kudzakhala kuli kulira, kusisima, ndi kukukuta kwa mano. Inu mudzaponyedwa mu hade, kumene nyongolosi siimafa konse kapena moto sumazimitsika, ndipo inu muzidzazunzidwa kupyola mu mibadwo yonse imene ili nkudza. Yesu ananena zimenezo. Icho ndi chithunzi chokuda, koma ndi chimene Baibulo linanena.

46 Ngati Mulungu analiweruza tchimo chotero nkukhala kuti ilo linatengera mtengo woterowo, zidzakhala ziri zotani ngati mizimu yosalungama iyo ikanati idzamasulidwe konse kachiwiri? Ife tikanadzakakhala nacho chinthu china chonga ife tinali nacho mu zaka sikisi sauzande zapitazo. Nkulondola uko? Sipakanadzakhala konse mwayi kachiwiri.

47 Tsopano inu mukuti, "Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti pamene iwe upita kumanda iwe—iwe umapita ku hade." Thupi lako limapita ku hade, uko nkulondola. *Hade* imatanthauza "kulekana." *Imfa* imatanthauza "kulekana." Thupi lako limafa, kulekana. Iwe umachoka kwa okondedwa ako kuno, koma si zomwe ife tikuzinena ayi. "Kunaikidwa kamodzi kwa munthu kuti afe, ndiye pambuyo pa izo, chiweruzo." Mwaona?

48 Tsopano, pamene iwe uli—ngati iwe uli woti ukayime pa chiweruzo cha Mulungu, iwe udzakaweruzidwa ndi Mulungu wokwiya. Ndipo Mulungu adzati—walengeza kale chimene Iye ati adzachite. Chotero inu mukudziwa chimene chiweruzo chanu chiti chidzakhale ngakhale inu musanakafike uko. Chotero chinthu choti nkuchita ndi kuti ukhale wopulumutsidwa ndi kukhala nacho chinthu chaulemerero ichi . . .

49 Penyani. Ngati ine ndimayenera kuti—ngati mzimu wanga . . . Penyani, sindife chinachake chakufa; ndife amoyo. Ngati—ngati wanga—ngati desiki ili pano—ngati thabwa ili likanakhala nao moyo umene uli mu chala changa, desiki ilo, ndi kukhala nalo luntha kuti lizirisuntha ilo, ilo likanakhoza kumasuntha monga chala changa chimasunthira. Ife sitiri opangidwa ndi zinthu za mtundu woterowo. Ife tiri opangidwa n—n—n—ndi makungu, ndi moyo, ndi minyewa; ndipo pali mzimu umu umene umalamulira izo zonse. Ndipo tangoonani kufulumira kwake momwe chikumayenera kuyenda. Tayang'anani kuno; dzanja langa likukhudza icho. Tsopano, posakhalitsa . . . Payenera kuti pakhale kuchitachita kokana ndi kovomereza. Mwamsanga pamene chala changa chikukhudza icho, icho chikumverera icho? Mwamsanga chotero izo zikupita ku malingaliro anga, ndipo malingaliro anga akuti, "Icho ndi chozizira," ndi kumapita mmbuyo. Mukuona kufulumira kwake izo ziri? Kufulumira kuposa ganizo, kufulumira kuposa chirichonse, ndi mchitidwewo apo. Nchiani icho? Muli chinachake chamoyo mmenemo, ndipo msempha uwo umagwira ntchito pa malingaliro. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Msempha umachikhudza icho, umachimverera icho, ndipo umanena kwa malingaliro, "Icho nchozizira." Malingaliro amati icho nchozizira, chifukwa icho chamvereredwa ndi msempha. O, mai! Inu mukakamba za mapangidwe.

50 Ndiyeno—zonse izo . . . Kufulumira kwake momwe Mulungu amadziwira ganizo lirilonse limene ife timalinganiza. Chirichonse chimene ife timachichita, Iye amachidziwa icho.

Chotero pamene wokhulupirira afa, iye amapita mu kukhalapo kwa Womupanga wake, Mulungu wake. Ndipo wochimwa, pamene iye amwalira, amapita kokafika kwake. Ndiye pa kubwerera . . . Tsopano, ine ndikuyankhula tsopano za Osankhidwa.

51 Koma alipo ena omwe ati adzatulukire mu chiukitsiro chachiwiri, omwe ati adzaichite kuima mu chiweruzo ndi wochimwa, kuti adzaweruzidwe limodzi ndi iye. Ine ndikufuna kuti ndikhale wotsimikiza kuti muchimvetse icho. Mwaona?

52 Tsopano, padzakhala pali . . . Choyamba chimene chiti chidzachitike chidzakhala k—kudza kwa Mkwatibwi. Padzakhala anthu mu dziko . . . Ine . . . Inu mukhoza kusiyana nazo pang'ono izi, koma mvetserani mwatcheru. Kungoti chifukwa inu munamulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanu wanu, izo sizitanthauza kuti inu muli kupita mu mkwatulo. Uwo ndi wa Osankhidwa, omwe ati adzapite mu mkwatulo. Padzakhala otsalira adzasiyidwe pa dziko lapansi pano amene ati adzapyole mu chizunzo ndi chisautso chachikulu. Mpingo udzakwatulidwira mmwamba mu mkwatulo.

53 Ndi akazi angati muno amene sadziwa kuti pamene inu mukuti mudule gawo la nsalu inu mumaiyala nsaluyo monga chonchi, ndi kuyala pateni yanu pa iyo monga chonchi, ndipo inu mumaidula nsaluyo molingana basi ndi pateniyo. Nkulondola uko? Ndipo nsalu ina yonseyo ndi ya mtundu womwewo basi wa nsalu iyo imene ili mu pateni. Nkulondola uko? Koma uwu ndi mtundu umene inu mumautenga. Inu mukhoza kuyiika iyo patali kuti mudzagwiritse ntchito mtsogolo, koma n—nsalu imene inu mumaidula apoyo . . .

54 Tsopano, mndani amayiika pateniyo? Mulungu, mwa kusankha. Ameni! Mulungu mwa kusankha amayika pateni. Iye anati, "Tsopano, ine ndinasankha asanaikidwe maziko a dziko . . . Ine ndawaika awa . . . " Chifukwa, Yesu anawauza ophunzira kuti Iye anali ndi iwo, ndipo Iye anali atawasankha iwo, ndipo anawadziwa iwo asanaikidwe maziko a dziko konse. Nkulondola uko? Chotero Mulungu amakhazika pateni. Tsopano, padzakhala Osankhidwa amene ati adzapite mu mkwatulo. Ndipo padzakhala gulu la anthu amene ali abwino, owongoka, okhala mwachiyero, anthu opulumutsidwa ndi Mulungu, amene sadzakhalapo mu mkwatulo; ndipo iwo adzatulukira mu chiukitsiro chachiwiri, chifukwa . . .

55 O, i—ine ndikuyembekeza inu simundikwiyira ine ngati ine ndingopanga chinachake momveka kwenikweni pano kwa inu. Mwaona? Musati mutero. I—ine ndiyenera kuti ndichinene icho, chifukwa ine—chikungopitirira kumanditsamwitsa ine (inu mukuona?) kuti ndichinene icho. Penyani. Tsopano penyani. Ndiye, ine ndikuti ndinene ichi: Alipo anthu omwe amakhulupirira kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro (mwaona?), ndipo iwo amakhala moyo wabwino, woyera, wopatulika; iwo amakhulupirira kuyeretsedwa naponso, kulandila . . .

56 Tayang'anani pa Yudasi Iskarioti. Yudasi Iskarioti analungamitsidwa pamene iye anakhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu ndipo anamulandira Iye ngati Mpulumutsi wakewake—Yudasi Iskarioti. Yudasi Iskarioti anayeretsedwa mu Yohane 17:17 ndipo anapatsidwa mphamvu mu Mateyu 10 kuti apite kunja ndi kukatulutsa ziwanda. Ndipo Yudasi Isikarioti anabwerera, iye atatha kuchiritsa odwala ndi kutulutsa ziwanda, ndipo iye anabwerera akusangalala ndi kumafuula mochuluka basi monga woyera wodzigudubuza wabwino aliyense yemwe munayamba mwamuwonapo. Nkulondola uko? Baibulo limanena chomwecho. Koma pamene iye anadza ku Pentekoste, iye anasonyeza maanga ake. Tsopano upenyeni uwo—mzimu umenewo.

57 Alipo anthu mu dziko lero, anthu abwino Achikhristu amene akhoza kukhulupirira mu kulungamitsidwa, ambiri a iwo, zikwi, mamilioni amene amakhulupirira mu kulungamitsidwa. Koma iwo alibe chochita ndi kuyeretsedwa. Ife tikanati awo

ndi Achipresbateria, Achiepiscopaliani, ndi ena otero. Iwo amakhulupirira mu kulungamitsidwa; amalalika izo. Ndipo izo nzabwino; iwo akulondola.

58 Koma tsopano, a—a Nazarene, Pilgrim Holiness, Free Methodist amasunthira mmwamba mu kuyeretsedwa. Iwo amakhulupirira mu kuyeretsedwa. Mokhoza! Iwo akulondola. Ndipo iwo amapeza chigonjetso, ndipo amafuula, ndi kuwatamanda Ambuye. Iwo akukhoza; iwo akulondola. Koma ukayankhula kwa mmodzi yense wa iwo za ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi mphamvu, ndi zizindikiro, ndi zodabwitsa, iwo amasonyeza maanga awo apo pomwe. Amati, "Ine sindikufuna chirichonse cha izo. Ine sindimakhulupirira . . ." Chabwino, ngakhale kwa anthu anga abwino Achinazarene, amakhulupirira kuti munthu yemwe amayankhula mu malirime ndi wa mdierekezi. Ndipo, m'bale, inu mukachita izo, inu . . .

59 Chifukwa, iwo amamuika Dr. Reedhead kunja kwa Mamishoni a ku Sudan, purezidenti wa iyo, chifukwa chakuti iye anayankhula ndi malirime. Anati, "Ife sitingakhoze kukhala ndi zimenezo."

60 Ine ndinati, "Inu simungakhoze kumalalikira monga Paulo ndiye. Inu simungakhoze kuulandira Uthenga wa Paulo, pakuti Paulo anati, 'Musamakanize ayi kuyankhula ndi malirime.'" Ndiko kulondola. Koma iwo—iwo amati ndi za mdierekezi. Iwo awona zonamizira zambiri, ndipo amazitengera izo konsekonse uko. Mwaona? Koma uwo ndi mpingo wolungamitsidwa ndi woyeretsedwa; koma amakana nati ubatizo wa Mzimu Woyera ndi ntchito yosiyana kwa kuyeretsedwa. Koma iyo ndi—iyo ndi ntchito yosiyana. Ndithudi iyo ili.

61 Panali zinthu zitatu zinabwera kuchokera mu thupi la Khristu. Ndipo zinthu zomwezo zimene zinabwera kuchokera mu thupi Lake ndi zomwe ife timazigwiritsa kuti tilowe mu Thupi Lake. Panali madzi (nkulondola uko?), Magazi (nkulondola uko?), ndi Mzimu. Ndipo Yesu, Lemba linati. "Alipo atatu amene amachitira umboni Kumwamba, Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Atatu awa ali Mmodzi; iwo ali Mmodzi. Koma zilipo zitatu zimene zimachitira umboni mu dziko lapansi; izo siziri chimodzi," iye anati, "koma izo zimagwirizana monga chimodzi: Madzi, Magazi, ndi Mzimu." Nkulondola uko?

62 Tsopano, inu simungakhoze kukhala nao Atate popanda kukhala naye Mwana. Inu simungakhoze kukhala naye Mwana popanda kukhala nao Mzimu Woyera, chifukwa—koma inu mukhoza kukhala olungamitsidwa popanda kukhala oyeretsedwa. Ndipo inu mukhoza kukhala zonse wolungamitsidwa ndi woyeretsedwa ndipo nkusakhala naobe ubatizo wa Mzimu Woyera. Mwaona? Izo nzoona. Ndilo Lemba. "Zitatu izi," iye anatero, "zimene zimachitira umboni mu dziko lapansi, madzi, Magazi, ndi Mzimu; ndipo izo zimagwirizana mu

chimodzi." Mwaona? Izo siziri chimodzi, koma zimagwirizana mu chimodzi, chifukwa ndi Mzimu womwewo mwa muyezo. Mulungu amatipatsa ife Mzimu mwa muyezo.

63 Tsopano, Lutera, pansi pa kulungamitsidwa, ndicho chimene iye ankalalikira. Nkulondola uko? Lutera ankalalikira, "Olungama adzakhala moyo mwa chikhulupiriro." Iye anali ndi uthenga waukulu. Ndipo ilo linali gawo la Mzimu Woyera. Ndiye Lutera, pamene Uthenga unabwerapo—Mulungu anali woti audzutse Mpingo Wake ndi kuutumiza Iwo kunja mokulirapo (o, mai!), Lutera anati, "O, ife tikukhulupirira ife tiri nazo Izo pano."

64 Koma John Wesile anati, "O, ayi!" Iye ndi George Whitefield ndi enawo, iwo anati, "Ife tikukhulupirira mu kuyeretsedwa, ndiyo, ili ntchito yachiwiri yotsimikizika ya chisomo." Nkulondola uko? Ndipo iwo ankalalikira Magazi. Chabwino, ngati Lutera sankafuna kuti asunthe, Mulungu anangozipereka izo kwa Achimethodisti a Wesile. Mwaona? Ndipo iwo anali nazo izo. Ndipo iwo anali nacho chitsitsimutso chimene chinasesa pa dziko, ndipo Mpingo weniweni.

65 Chabwino, tsopano, pamene nthawi iyo yabwerapo... Tsopano, motsatira padza umboni wa Mzimu Woyera wa zizindikiro, zodabwitsa, ndi zozizwitsa. Tsopano, Wesile sakufuna kuti agwirizane ndi izi. Tsopano, ngati Wesile akanakhala pa dziko lapansi ndipo Marteni Lutera akanakhala pa dziko lapansi pa nthawi izi, iwo akanati agwirizane nazo izo, koma iwo angokhala ndi pafupi kuzungulira kwachiwiri k—k—kwachinai kapena kuzungulira kwachisanu kwa atumwi kwapita mu izo, ndipo iwo anangozisodza izo zonse nkutha.

66 Tsopano, Achipentekoste anazilandira ndipo anakhulupirira kuyankhula mu malirime. Ndiye iwo anazisandutsa izo kukhala "umboni woyambirira," kuti aliyense ayenera kumayankhula mu malirime. Uko ndi kulakwitsa. Koma tsopano—tsopano iwo abwereranso... Izo zinali zibadwa zoperekedwa ndi Mulungu. Basi monga ine sindingakhoze kudzithandiza, chifukwa ine ndiri ndi maso a buluu, kapena... Mulungu anangondipatsa ine. Iyo ndi mphatso Chabe mu Mpingo. Mulungu anaziyika izo mmenemo. "Mulungu waika mu Mpingo..." Mwaona?

67 Tsopano. Koma pamene iwo anabwerapo ndi izo... Tsopano, iwo anali ndi dalitso lalikulu, anapita patali kupyola Achilutera kapena Amethodisti, aliyenseyo. Ndipo tsopano, iwo apanga bungwe mwanjira yotero mpaka iwo ali moipa kuposa Amethodisti ndi enawo—Achipentekoste. Ndiyeno, iwo afika pamalo amene kuzungulira kwachiwiri ndi kwachitatu... Zakhala ziri pafupi zaka makumi anai kuchokera pamene iwo anayamba kulandira kuyankhula mu malirime. Koma mtengo uwu wa Mulungu uli ndi zipatso zisanu ndi zinai zosiyana pa iwo. Tsopano, chirichonse cha zipatso izi inu mungakhoze

kukhala nacho. Mwaona? Mulungu wazitumiza izo, koma zonse palimodzi zikuchokera mu mtengowu.

Tsopano, kulungamitsidwa, tayang'anani pa iko.

68 Tayang'anani pa phunziro la mmawa uwu. Pamene chiweruzo chinaikidwa, ndipo mabuku anatsegulidwa... Tsopano, Yesu anadza ndi zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi za oyera, ndiyeno chiweruzo chinaikidwa. Apa iwo onse ali kuzungulira Mpandowachifumu Woyera wa chiweruzo (monga ife tinapita kudutsa mu Lemba ndi izo), ndipo mabuku anatsegulidwa; ndipo Bukhu lina linatsegulidwa limene linali Bukhu la Moyo. Ndipo awa a mu mkwatulo anali kuwaweruza awo. Nkulondola uko? Iwo amene anali atapita kwao ndipo atalandira matupi awo aulemerero, nakhala moyo kudutsa mu Zakachikwi, analipo apa mu Chiweruzo cha pa Mpandowachifumu Woyera, kumawaweruza enawo. Iye anati Iye akanati adzalekanitse nkhosa kwa mbuzi.

Tsopano, inu mukuti pano, "Chifukwa, tsopano penyani." Inu mukuti, "Kodi awo akubwerapo...Kutiko, M'bale Branham?" Mu chiweruzo cha Mpandowachifumu Woyera.

69 "Nanga bwanji mu mkwatulo?" Chabwino, mu nthawi ya mkwatulo...Yesu anaphunzitsa izo ngati fanizo. Ndipo Iye anaphunzitsa izo mwanjira zambiri zosiyana. Nayi njira imodzi. Iye ananena kuti panali anamwali khumi anatuluka kuti akakomane ndi Ambuye. Ndipo anawona-...Onse awo anali anamwali, koma ena anali ndi Mafuta mu nyali zawo ndipo enawo analekerera Mafuta atheretu. Nkulondola uko? Ndipo pamene Mkwatibwi...Tsopano, kodi Mafutawo anali chiani? *Mafuta* anali Mzimu Woyera; Baibulo linanena chomwecho. Tsopano penyani. Iwo anali anamwali. Tsopano, kodi *namwali* amatanthauza chiani? "Wopatulika, waukhondo, wolekanitsidwa, woyeretsedwa." Nkulondola uko?

70 Ngati ine ndikadakhala ndi galasi laling'ono pano ine ndikanakusonyezani inu chimene...Pano, mwa chitsanzo monga botolo ili pano, ngati ilo likanakhala lopanda kanthu, ndipo ine ndikanalitola ilo, ndipo ilo likanakhala lakuda basi monga ilo likanakhalira...Ine ndikufuna kuti ndiligwiritse ntchito. Chabwino tsopano, chinthu choyamba chimene ine ndikufuna kuti ndichite ndicho Kulungamitsa. Ine ndilitola ilo chifukwa ine ndikufuna kuti ndiligwiritse ilo ntchito. Ilo ndi lakuda; ine ndinalipeza ilo kunja mu—mu khola la nkhumba, kapena kumene ilo linali. Tsopano, ngati ine ndiri munthu wamtundu woyenera, chabwino, ine sindikufuna kuti ndiike chinachake choyera mmenemo ine poti ndichigwiritse ntchito. I—ine ndiyenera kuti ndichikonze chinthu icho poyamba. Tsopano, chinthu chopambana kuchichita ndicho kuliwawula ilo, kulitsuka ilo, ndi kuliyeretsa ilo. Kodi uko nkulondola? Tsopano, kodi liwu lakuti *kuyeretsa* limatanthauza chiani?

"Kutsukidwa ndi kuikidwa pambali kuti litumikire." Zotengera za kachisi wakale zinkatsukidwa ndi kuikidwa pambali kuti zitumikire.

71 Tsopano, pali Mpingo: Mulungu anawatenga iwo kupyolera mu m'badwo wa Lutera, kulungamitsidwa; m'badwo wa Wesile, Iye anawayeretsa iwo; ndipo mu m'badwo uno Iye akuwadzaza iwo. Mwaona? Iye akuika Moyo mwa iwo. Ndipo pamene uwu, Moyo Wake kupyolera mu Mzimu Woyera . . . Mzimu Woyera unawatenga iwo; Mzimu Woyera unawayeretsa iwo; Mzimu Woyera unawadzaza iwo. Mwaona? Wonse uwo ndi Mpingo womwewo.

Koma tsopano penyani. Tsopano mu tsiku lino . . .

72 Tsopano, ine ndikuganiza kuti Lutera, Wesile, ndi onse a iwo, ambiri a iwo adzapita mu mkwatulo. Iwo anali nalo gawo la Mzimu linalalikidwa kwa iwo; iwo analikhulupirira ilo.

73 Tsopano, mu mkwatulo . . . Alipo anthu lero amene anapita mu zipembedzo izo zimene sizinasunthire patsogolo. Ndi . . . Pakhala pali chipembedzo chimodzi chokha, ndicho Mpingo wa Mulungu; ndipo Iwo umangomasuntha chitsogolo chimodzimodzi basi. Koma mabungwe awa aphwasula zinthu izi monga choncho. Ndipo anthu ambiri lero amayang'ana pa ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kumati izo ndi zamkutu. Koma apobe iwo akhala atalungamitsidwa; apobe iwo akhala atayeretsedwa. Koma iwo amati, "O, uko ndi kutengeka, zinthu zimenezo."

74 Ine ndikudziwa mdierekezi ali nazo zowopysezera akhwangwala zamitundu yonse kunjako. Uko ndi kumene inu mumapezako ma apulo abwino, ndi kuzungulira pomwe zowopsyezera akhwangwala izo ziri. Ndiko kulondola. Ingopitirirani molunjika mkati kuseri kwa chinthucho, pitani muzikadya maapulo. Mwaona?

75 Tsopano, izi . . . Ndiye Mulungu anaudzaza ndi Mzimu Woyera . . . Ndiye Iye anawuika Mpingo Wake kunja kuti awupatse Iwo ulemerero. Pa kudza kwachiwiri, apa pakudza Mpingo kubwerera, Mkwatibwi. Tsopano penyani. Muone ngati iwo akupyola mu nthawi ya chisautso. Iye anati, "Anamwali awa, amene anabwera ndipo anati, 'Tipatseniko ife ena a Mafuta anu.'"

"Mkwati akudza!" Mfuu unamveka uko, "Taonani, Mkwati akudza. Pitani inu kunja kuti mukakumane ndi Iye."

Ndipo anamwali awa, amene anali anamwali, oyera, opatulika (taganizani za izo), anthu oyera, opatulika opanda ubatizo wa Mzimu Woyera, iwo anati, "Tipatseni ife Mafuta!"

76 Ndipo Mpingo unati, "Ife tangotsala ndi otikwanira ife tokha. Inu pitani mukapemphere mokwanira." Koma ndi mochedwa apo. Chotero, mpingo unapita nukalowa mu Ukwati,

ndipo ena awa anaponyedwa mu mdima wakunja (nkulondola uko?), kumene kunali kulira ndi kusisima ndi kukukuta kwa mano; ndipo iwo anadutsa mu chinzunzo, anavutika, anafa.

77 Yesu anabwereranso ku dziko lapansi. Ulamuliro wa Zakachikwi unayambitsidwamo, zaka chikwi ndi Iye. Atauka anabwera—olungama ndi osalungama. Ndipo Iwo anamuweruza munthu aliyense. Ndipo mbuzi zinali ku mbali imodzi ndi nkhosa ku mbali inayo. Ndiyeno Mulungu anabwera ndipo anadzautengera Mpingo namka pa dziko lapansi lonse ku msonkhano wamisasa, kumene ife tonse tidzakasonkhana limodzi ndi okondedwa athu. Mwaona? Uko ndiko kusiyanako.

78 Tsopano, anthu awa pano . . . Ndithudi pamene ife tifa, ngati ife tiri mwa Khristu Yesu, ife timapita kukakhala ndi Thupi lalikulu ilo kutaliko, Khristu Yesu. Ngati ife tiri ochimwa, ife timapita kukakhala ndi thupi lalikulu ilo la osakhulupirira; ndipo Mulungu anati gawo lathu linali ndi onyengawo, ndi ena otero, mu hade. Ameni! Mwina sizingakhoze kukhala ndendende zomveka.

Koma, tiyeni ife tione tsopano ngati ife tingakhoze kupeza . . . Kolembedwa kakang'ono chabe pano.

16. Chonde fotokozani Eksodo pa 24—mutu wa 4 ndi ndime ya 24. Kodi Lemba ili limatanthauza chiani—kuti Mulungu ankati amuphe Mose kapena mwana wake? Ndi chifukwa chiani?

79 Ife tikudziwa pamene izo ziri, Eksodo 4:24. Ilo ndi funso labwino. Tsopano, pano ife tiziwerenga izo pomwe pano mphindi yokha. Eksodo 4 ndi 24:

> *Ndipo izo zinafika pochitika cha ku njira ya ku nyumba ya alendo, kuti* AMBUYE *anakomana naye iye, ndipo anafuna kuti amuphe iye.*

Ndi angati akuikumbukira nkhaniyo? Tsopano, Mulungu anamupatsa Abrahamu, mibadwo Mose asanakhalepo, chizindikiro cha mdulidwe. Ndipo ilo linali pangano limene Mulungu analipanga, kuti Myuda aliyense ayenera kuti azidulidwa. Nkulondola uko? Mwamuna aliyense ayenera kuti . . . Icho chinali chizindikiro.

80 Ndipo kodi ife timadulidwa lero? Ndi Mzimu Woyera, osati mwa thupi.

81 Tsopano. Tsopano, Mulungu anapereka lamulo ili, "Ndipo mwamuna aliyense ayenera kuti azidulidwa." Ndipo Mulungu, pamene Iye anamuitana Mose kuti apite kumusi uko ndi kukawapulumutsa ana a Israeli, Mose anali asanachite pa mwana wake chizindikiro cha chiombolo chomwe. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

82 Zikadakhala ngati ine kumati, "Inu nonse mpingo tsopano, aliyense wa inu—inu mubwere ndi kudzabatizidwa ndi madzi,

ndipo ife tikuikani inu pa umembala wa mpingo. Ife tonse tipita ku ulemerero palimodzi." Bwanji, m'bale, awo si Malemba ayi. Kupatula inu mutabadwa kachiwiri, odulidwa ndi Mzimu Woyera . . . Inu muyenera kuti mukhale. Ine sindikusamala kaya ndinu abwino motani, ndinu a mpingo wuti, momwe makolo anu analiri abwino, kupatula inu monga wapayekha mutabadwa kachiwiri ndi Mzimu Woyera, inu simudzapita konse mu mkwatulo. Mwaona? Inu simungakhoze kupita. Ndicho chizindikiro chomwe chachiwombolo, mdulidwe; ndipo mdulidwewo uli mwa Mzimu Woyera. Tsopano Mulungu . . .

83 W—wofunsayu anafunsa izi: "K—kodi Lemba ili likutanthauza kuti Mulungu analinga kuti amuphe Mose kapena mwana wake? Ndipo chifukwa chiani?" Mulungu ankamufuna Mose. Ndipo Zipporah anali yekhayo yemwe anamupulumutsa iye apo. Pakuti Zipporah anatenga mwala wakuthwa, ndipo anapita, ndipo anakadula khungu la nsonga ya mwana wake, ndipo analiponyera ilo pamaso pa Mose ndipo anati, "Iwe ndi mwamuna wamagazi kwa ine." Nkulondola uko?

84 Ndipo Mulungu akadautenga moyo wa Mose, koma mwina Mngelo anali ataima apo, ndipo anati, "Zipporah! Chigwire icho mwamsanga!" Mwaona?

85 Ndipo Zipporah anakamudula mwanayo. Anati, "Mose, ndiwe wo—wokhudzidwa kwambiri ndi zina zirizonse ndi za ulendo wako, koma mnyamata wako yemwe si wodulidwa."

Ine ndimangodabwa nthawi zambiri ngati . . . Nthawizina ine ndakumana ndi anthu amene amati, "O, ulemerero kwa Mulungu. Ambuye akufuna ine kuti ndichite chinthu *chakuti*. Iye akufuna ine kuti ndipite ku Afrika, ku India."

86 Ine ndimati, "Kodi inu munayamba mwamufunsapo munthu wa mkakayo ngati iye anapulumutsidwa? Kodi inu munayamba mwamufunsapo mnyamata wa manyuzi ngati iye anabadwa kachiwiri kale? Nanga bwanji oyandikana nanu, kodi iwo anapulumutsidwa?" Mwaona? Tsopano, ndilo funso. Mwaona? Ngati izo ziri mu mtima mwanu . . .

87 Kuno nthawi ina kalelo mkazi anakumana nane kumusi kuno mu Florida. Ndipo mkazi wamng'onoyo, ine ndiribe njira . . . Sindine woweruza. Koma pali mlaliki wamng'ono anali komwe kuno ndipo anadzalalikira pa nsanja pano. Ndipo mnyamata wamng'onoyo mu dziko lina anali wokwatira ndipo anali ndi mkazi, ana atatu kapena anai. Ndipo mkazi uyu anali mayi wamasiye. Ndipo iwo anabwera kuchokera ku Texas, limodzi mpaka kuno mu galimoto yaikulu ya Cadillac. Ndipo mkaziyo anabwera nalowa. Ndipo iye ali ndi ufulu woti avale mulimonse momwe iye amafunira kutero, sizinapange kanthu kwa ine; koma monga Mkhristu wachikazi iye sanavale basi mokhala ngati icho. Iye anali (o, mai!)—iye anali—anali ndi zazikulu kwambiri zazitali—ndolo zammakutu izo (kaya zomwe

inu mumazitcha izo) zikulendewera pansi monga chonchi, ndipo iye anali ndi kwenikweni zambiri z—za zinthu pa kamwa pake; n—n—ndipo nsidze zake zinali zitametedwapo ndipo anali ndi nsidze zina, ndi pensulo, atazipaka apo. Ndipo iye anati, "M'bale Branham," anati, "Ambuye akundiitanira ine ku dziko lachilendo."

Ine ndinati, "Iye ali?"

"Inde!" Ndipo iye anati, "Inde ndikupita uko ndi bambo uyu."

Ndipo ine ndinati, "Chabwino, ngati Ambuye akukuitanani inu, chabwino, nzabwino." (Koma ndi chipatso chawo... Sizinkawoneka mochuluka kwambiri kwa ine ngati... Mwaona?)

Ndipo iye anati, "Kodi inu simukuwakhulupirira Ambuye...?"

88 Ine ndinati, "Tsopano, musati mundifunse ine. Ngati Ambuye akuuzani inu, inu muchite chimene Ambuye akuuzani inu kuti muchite. Koma kwa ine, ine sindikuganiza chomwecho, kwa ine ndekha. Ine ndingokhala woonamtima ndi inu."

Iye anati, "Chabwino, chifukwa chiani inu mukuganiza chomwecho?"

Ine ndinato, "Chinthu choyamba, monga inu ngati mkazi wokwatiwa ndi mwamuna wokwatira uyu sizikuoneka zabwino kwambiri, inu kumakhala kumusi kuno mu mzindawu limodzi. Ngati chirichonse chimabweretsa chitonzo ndi zimenezo. Mwaona?" Ndipo ine ndinati, "Tsopano, chinthu choyamba..."

89 Tsopano, nchiyani chinachitika kwa mkazi ameneyo? Chinthu chomwecho chikanati...Iye anakhala akudzidetsa kumeneko pokhala wosalandira Mzimu Woyera, basi monga mkazi wa kutali uja lero yemwe anandiitana ine ndipo amafuna kuti akwatiwe ndi mwamuna uja, ndi kumusiya mwamuna wake yemwe, ndi kukwatiwa ndi mwamunayo. Iye anali atafika mu malo oterewo, mwina nthawi ina anakhudzanapo ndi Mulungu, koma anali akusirira zinthu za mdziko. Ndipo ine ndinamufunsa iye; ine ndinati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera?"

Iye anati, "Sindinati panobe, koma ine ndikuufunafuna Iwo."

90 Ine ndinati, "Inu mulandire Mzimu Woyera poyamba, ndipo Iye adzakuuzani inu mwamuna yemwe muyenera kukhala naye." Ndiko kulondola. Mwaona?

I—inu muyenera...Ndi chimene icho chiri. Ngati inu simutero, inu mufa mwauzimu. Mulungu akufunafuna zochuluka usikuuno, mwakuti Iye wagogoda [M'bale Branham akugogoda pa guwa—Mkonzi.] pa mtima wawo nthawi zochuluka kwambiri. Ndipo imodzi ya nthawi izi Iye adzachitseka chitsekocho, n—ndipo chifundo chapita. Mwaona?

91 Ndithudi, Mulungu akanautenga moyo wake. Iye anati Iye anamufunafuna iye. Tamverani momwe Lembali likuwerengekera:

> *Ndipo zinafika pochitika cha pa njira ya ku nyumba ya alendo, kuti* YEHOVA *anakomana naye iye, ndipo anafuna kuti amuphe iye.* (Mose. Tsopano penyani.)
>
> *Ndiye Zipporah anatenga thanthwe lakuthwa—mwala wakuthwa, ndipo anadulapo nsonga ya khungu la mwana wake, ndipo anaiponyera iyo pa mapazi ake, ndipo anati, Ndithudiiwe uli mwamuna wamagazi kwa ine.*

92 Ndiko kulondola. Tsopano, Mulungu sanali kufunafuna mwanayo. Mulungu . . . khanda laling'ono losauka ilo silinkadziwa choti nkuchita; ilo ndi losalakwa. Koma chimene chinali, anali bambo wa mwanayo, yemwe anali kumutengera mwanayo kupita uko kuti akawaombole ana a Israeli pansi pa chizindikiro cha mdulidwe; ndipobe mwana wake yemwe anali asanadulidwe nkomwe. Mwaona? Ndipo Zipporah anadula iyo ndi mwala, nsonga ya khungu, ndi kuiponyera iyo pansi, ndipo anati, "Iwe ndiwe mwamuna wamagazi kwa ine."

17. Chonde fotokozani matanthauzo a Lemba, ndi pamene ilo liti lidzafike pokwaniritsidwa: Yesaya 4 ndi 1. Zikomo.

Chabwino. Ife tingotembenuzira apo tsopano . . . Anthu inu amene muli ndi Mabaibulo anu ndipo mukufuna kutero . . . Ife tiona chimene Ine sindinakhoze kupeza mwayi woti ndiliyang'ane ili, koma ine ndimaganiza mwina ife tikanapeza mtundu wina wa yankho. Pano ife tiri.

> *Ndipo mu . . .* (O, eya!) Ndipo izo zidzachitika . . . *Ndipo mu tsiku limenelo akazi asanu ndi awiri adzamugwira mwamuna mmodzi,* ndipo adzati, *Ife tizidya zakudya zathu zathu, ndipo tizivala zovala zathu zathu: utilole kokha ife tizitchedwa dzina lako, kuti utichotsere chitonzo chathu.*

93 Chabwino, m'bale, izo ziri pafupi zedi moipa chotero tsopano. Kugwera kunja kwake kumene kwachitika kwa dziko lathuli! Ndiroleni ine ndinene ichi, abwenzi anga okondedwa a Chikhristu. Ndiroleni ine ndinene ichi ndi kulemekeza kwaumulungu kwa aliyense: Ngati kunayamba kwakhala konse . . . Ndipo anthu inu muno amene mwaphunzira mbiriyakale, ife tiri pa msewu womwe pamene fuko lirilonse labwino kupyola mu mibadwo linagwerapo, kuonongeka chikhalidwe, kubwerera mmbuyo komwe.

94 Monga ine ndinanena mmawa uwu . . . Mundikhululukire ine pobwereza izi. Mu maiko achilendo amuna amadza kwa ine ndipo amati, "M'bale Branham, ndi akazi a mtundu wanji omwe inu nonse muli nawo kumeneko? Chabwino, nyimbo zonse zomwe mumaziimba, tinyimbo tina tonyansa tokhudza akazi

anu." Ndi zimenezo. Onse amaimba chisokonezo china cha—cha—cha . . .

95 Chabwino, kodi inu mukudziwa chimene icho chiri? Ngati inu mukufuna kuti ine ndikuuzeni inu mu mawu ochepa, ine ndikuuzani inu ndendende. Dziko lafika mu chikhalidwe cha mtundu umenewu, chifukwa ndi Sodomu ndi Gomora wamakono. Ndendende! Mu California ine ndinatenga nyuzi. Ndipo ine ndaiwala kuti ndi zikwi zingati chaka chirichonse zimene iwo amazigwira, kuti adziwe, za kuchuluka kwa amuna ogonana. Ngakhale chilakolako chawo chachibadwidwe cha—p—pakati pa mwamuna ndi mkazake, ndi zina zotero, chakhala chikuwachokera anthuwo. Ndendende chimene Mulungu anati chikanadzafika pochitika. Ndi zao zomwe . . .

96 Inu mudzatengepo ina . . . Muone yemwe amapeza mtundu wina wa kutchuka. Kamvetsereni pa wailesi yanu, kapena televizioni, kapena chirichonse chimene inu muli nacho, ndi kukazipeza. Ndi choipa kwambiri ndi chonyansisitsa . . . Pakakhala nyimbo ina yokhudza mkazi wina kapena chinachake chonga izo, ndi chinthu chimene chimatenga kutchuka.

97 Ndipo izo zafika pa malo pamene izo zikunga ngati kuti ife sitikusamala za akazi athu—kapena akazi athu sakudzisamalira okha. Ndi chimene chiri. Ngati mkazi akanamadzisunga yekha mwaubwino, mwamuna akanakhala akuyenda mwaubwino. Ndipo uko si kumutengera mbali mwamuna, koma ine ndikudziwa icho ndi choonadi. Inde, bwana! Koma ndi chiani icho? Ndi basi—chikhalidwe choipisitsa, ndipo chikungokhalapo basi. Ndipo chiri molingana ndi Lemba. Baibulo linati izo zikanamadzakhala ziri mwanjira imeneyo. Chotero ife tingakhale nacho bwanji chitsitsimutso? Ife tingakhale nacho motani chitsitsimutso?

98 Mvetserani, abwenzi Achikhristu. Mu mphindi zochepa zatsalirazi ndiroleni ine ndikufunseni inu chinachake. Ife tiri naye Billy Grahams. Ife tiri ndi Jack Shuler. Ife tiri ndi mitundu yonse yosiyana ya mayendetsedwe a zipembedzo zikupita kudutsa mdzikoli. Ndipo iwo akhala akupita kwa zaka sikisi kapena seveni zapitazi kudutsa United States molimba monga iwo angathe kuyendera, ndipo palibe chitsitsimutso. Chifukwa? Zitseko zikutsekeka. Ife takokolola nsomba iliyonse, monga ine ndinanena mmawa uwu, kuchokera pa dziwe. Mwina imodzi kapena ziwiri zakakamira penapake.

99 Kumene Billy Graham anali ndi msonkhano (ine ndikukhulupirira uko kunali ku Boston kapena kwinakwake), ndipo iwo amati iwo anali ndi otembenuka zikwi makumi awiri ndi zinazake mu masabata sikisi. Iwo anabwererako masabata angapo pambuyo pake ndipo sanakhoze kukapeza makumi awiri. Taganizani za izo! M'bale, izi zangotsala

pang'ono kutsirizika. Ine ndikadakhoza kunena chinachake pano. Mwaona?

100 Ife tikukhala mu masiku amene Mulungu anati akanadzabwera. Ndipo ife tikukhala mu masiku otsiriza. Ndipo ife tikukhala mu nthawi imene amuna . . . Mosasamala momwe ife tikuyesera kuganizira za izo, Mawu a Mulungu amanena kuti ife tiri okonzedweratu. Ndiko kulondola. Ndipo amene Mulungu wawaitana abwera kwa Mulungu; ndipo amene Mulungu sanawaitane sabwera kwa Mulungu. Mulungu amaitana, ndipo iwo amakana, ndipo Iye amaitana, iwo amakana. Tsopano, ine sindikunena kuti Mulungu akumuweruza aliyense. Iye sali kulolera basi kuti onse k—kuti aliyense awonongeke, koma onse akhoze kudza ku kulapa. Koma polinga kuti akhale Mulungu, I—Iye ankadziwa pa chiyambi kuti iwo sakanati adzabwere. Komabe Iye anawapatsa iwo mwayi, koma iwo sakanakhoza kubwera.

101 Bwanji . . . Ngati iye sakuzidziwa izo, Iye ankadziwa bwanji kuti ife tikanadzakhala ndi zikuku zopanda akavalo? Iye ankadziwa bwanji kuti nthawi zino zikanadzabwera monga ife tiri nazozi tsopano? Nchifukwa chiani Iye anati, "Anthu akanadzakhala ammutu, amaganizo apamwamba, okonda zokondweretsa"? Nchifukwa chiani aneneri onse ananeneratu zinthu zina zonse izi kuti zikadadzabwera kuchokera kuchiyambi komwe? Mulungu ankadziwa chirichonse. Iye amadziwa chimene chiti chidzakhalepo. Ndipo muli anthu mmenemo amene Mulungu anayang'ana pansi kupyola mu nthawi ndi kuti, "Awo sadzabwera." Ndipo iwo ali otsutsidwa basi ndi chitsutso icho, chifukwa iwo anazisankha izo okha. Ameni! Ndi inu apo.

102 Ndipo ine ndikukhulupirira, m'bale wanga, mlongo, (ine ndikunena izi ndi kulemekeza kwa umulungu ndi mantha a kwa Mulungu mu mtima mwanga), ine ndikukhulupirira Amereka wamira! Iye wayipa mmakhalidwe. Iye wapita pansi kufika potsikitsitsa. Ndi zachisoni.

103 Tangoganizani apa, monga ine ndikunena pa—pa kuyankha Lemba ili, akazi seveni kumugwira mwamuna mmodzi. Mu Nkhondo Yoyamba ya Dzikolonse—Nkhondo Yachiwiri ya Dzikolonse . . . Ine ndiri ndi c—chodula kunyumba chochokera mu nyuzipepala. Inu munaiwelenga iyo nokha. Anati, "Chachitika ndi chiani ku zikhalidwe za akazi athu Achimereka? Awiri mwa ankhondo atatu aliwonse anasudzulidwa ndi akazi awo pamene anapita kutsidya kwa nyanja mu miyezi sikisi yoyambirirayo." Awiri mwa atatu anasudzulidwa. Akazi awa anangochokapo napita kwina. Nchifukwa chiani izo? Ngati inu mungamvetse, abwenzi, ndi mzimu wa nthawiyi.

104 Ife tiyenera kuti tilowe mu mzimu wa masiku otsiriza pamene masiku otsiriza ali pano. Inu mukapita ku chipinda

chovinirako, inu mumayenera kuti mulowe mu mzimu wa kuvinako, kapena iwo sati avine. Inu mukapita ku tchalitchi, inu mumayenera kuti mulowe mu Mzimu wa kupembedza inu musanafike popembedza. Dziko liyenera kufika mu mzimu wa masiku otsiriza masiku otsirizawo asanabwere, ndipo ife tiri mu mzimu wa masiku otsiriza. Ndipo Mulungu analonjeza kuti zinthu izi zikanati zidzakhale pano, ndipo izo ndi zimene ife tiri nazo. Ife tiri mu masiku otsiriza. Ndipo amuna ndi akazi akadali mtulo ndipo sali kuzizindikira izo.

105 Ndipo makhalidwe . . . Ine ndinakomana ndi mnyamata wamng'ono kuno tsiku lina cha mu . . . o, nthawi ina pakale, kugwa masamba kwapitaku. Ndipo ife tinali kubwera mu mzinda. Ndipo iye anali kundiuza ine, mnyamata wamng'ono wa ku sukulu yapamwamba yemwe anali atakwatira. Iye anati, "Ine ndimukwatira msungwana uyu, chifukwa iye anali msungwana wabwino, ndipo ndinayenera kumukwatira iye, asanatsirize sukulu yapamwamba." Anati, "Ife sitinakhalepo naye mmodzi anapezedwa ali namwali, monga momwe ine ndikudziwira, mu sukulu yapamwamba kwa zaka kuzungulira kuno." Mwaona? Amakhalidwe oyipa basi.

106 Ndipo uko mu c—California ine ndinapita kudutsa mmisewu mu malo komwe apolisi amakhoza kukuuza iwe kuti uchoke mu msewuwo. Ndi kowopsya kwambiri mwamuna kuti azidutsa mu msewu kuposa momwe zikanakhalira ndi mkazi. Njira zamdima. O, Mulungu, chitani chifundo! Kodi inu simukudziwa kuti Baibulo linanena kuti zinthu zimenezo zikadadzabwera?

107 Ndipo basi Iye asanapereke mthunzi wake mu Sodomu ndi Gomora, ndipo anapita kumusi uko, chinthu chomwecho kuchitika—chinachitika, kani. Ndipo Mulungu anatumiza moto pansi ndipo anawatcha malowo kotheratu. Chikwangani chomwe choti chisonyeze kuti dziko konse, pamene ilo lifika pa malo amenewo, likadati lidzalandire [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] chinthucho.

108 Ife tiri ku masiku otsiriza. Zedi. Akazi seveni kumugwira mwamuna mmodzi, nkumati, "Ife tizidya mkate wathu wathu ndi kumavala zovala zathu zathu, kungoti utilore ife tizitchedwa dzina lako kuti tichotse chitonzo chathu." M'bale, inu simukusowa kuti muchite kuchoka mu United States. Alipo malo amodzi okha amene ine ndawaonapo mu moyo wanga amene ine ndinaganiza kuti anali oyipirapo kuposa misewu ndi zinthu zimene ine ndakhalamo mu fuko lathu lomweli. Ndipo ife sitikufika pabwinoko mulimonse. Ife tikupitirapitira kukhala moipiraipirabe nthawi zonse. Ndipo kumbukirani, ine ndikuyankhula mu Dzina la Ambuye. Ife tipitirira kumamka moipira. Pali chiyembekezo chimodzi chokha ngakhalebe, ndipo icho chiri mwa Khristu Yesu. Ziribe kanthu zomwe mungachite.

109 Ine ndalira mofuula, ndapita kudutsa m'fukoli kuno. Ndipo Mulungu wadzutsa ngakhale akufa. Ndipo ife tapita mu mizinda; ndipo anthu amauka amene anakhala ali mu zikuku kwa zaka, ndi kumayenda kudutsa mu mzinda mmbuyo mwa magalimoto, akukankha zikuku zawo ndi zinthu monga choncho. Ndipo akazi, amene madokotala anena kuti amwalira, atanyamula ma X-ray awo ali ndi dzina la dokotala pamwamba pakepo, ataukitsidwa kwa akufa. Ndipo mzinda wonsewo nkukhala gada ndi kumati, "Unhu, zowerenga maganizo; gulu ka oyera odzigudubuza." O, inu simungakhoze kuyembekezera chinthu china chirichonse koma chilango! O! Kulondola uko!

110 Chiweruzo chiri pano, ndipo inu muyenera kuti muchilandire icho. M'bale, thawani ku mkwiyo uli mkudzawo ndi kupita kwa Khristu Yesu mwamsanga momwe inu mungathere! Chokani kwa zinthu izi! Inde, uwo ndi mzimu wa masiku otsirizawa. Zinthu zambiri zikanakhoza kunenedwa. Ine ndifulumire.

18. Kodi inu chonde mungatiuze ife momwe Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu akuyembekezera ife kuti tizibwerera mu nyumba ya Ambuye wathu kudzapembedza?

111 Chabwino, ilo ndi limodzi labwino. Ilo ndi lofunikira kwambiri kwa mpingo uliwonse. Mulungu amakuyembekezani inu kuti muzibwera ku nyumba ya mpingo . . . Tsopano, ilo ndi funso chabe, funso la kunja chabe. Ilo si la Mwamalemba; liri—komabe liri. Dikirani, ine ndikuuzani inu chimene Iye ananena. Malo oyamba, ngati inu mukufuna Lemba, anthu ayenera kuti azibwera ku nyumba ya Mulungu mwa cholinga chimodzi, ndicho kuti adzapembedze, kudzaimba nyimbo, ndi kudzamupembedza Mulungu. Ndi momwe Mulungu akuyembekezera ife. Iye samatiyembekeza ife kuti tizibwera mu nyumba ya Mulungu kudzayankhula za zathu—kapena chinthu chinachakenso, kapena kudzayankhula za wina ndi mzake, kapena kudzayankhula za zomwe ife tikuyenera kuti tizichite popyola mu sabata; Iye amayembekeza ife kuti tizibwera kudzampembedza Iye. Iyo ndi nyumba ya kupembedza. "Ndipo chirichonse chiyenera kumachitidwa mwaubwino ndi mwa dongosolo," anatero Paulo mu Baibulo. Chirichonse chikuyenera kuti chizikhala molongosoka. Pakuyenera kuti pakhale pali uthenga.

112 Chinthu choyamba ine ndikanati ndinene, molingana ndi malamulo a Mpingo mu Chipangano Chakale—kapena Chipangano Chatsopano kani, pa malo oyamba, anthu ankalowa mu mpingo wa—wa Mulungu mu Mzimu wa kupembedza. Ndipo iwo ankayenda kulowamo, nyimbo zinkaimbidwa. Ndipo mwina mlaliki ankakhoza kuyankhula, pakuti iye anali mneneri wa mpingowo. (Mneneri wa Chipangano Chatsopano ndi mlaliki; ife tikudziwa izo: "Umboni wa Yesu Khristu ndi Mzimu wa uneneri," amatero mu Chivumbulutso.)

113 Tsopano, mlaliki amayamba kulalikira. Pamene iye akulalikira, madalitso, apo pomwe, mwina kumapeto a ulaliki wake, amayamba kugwa; anthu amakhoza kunena, "Ameni," kumamka akumudalitsa Mulungu. Ndiye mwamsanga iye akangoti wasiya kulalikira, apo mwina pamakhala uthenga ukubwerapo, mwina mwa kuyankhula ndi malirime osadziwika (1 Akorinto 14:13, 14). Ndiye—ndiye ngati pakhala pali popanda wotanthauzira mu mpingo, munthu uyu amayenera kuti akhale chete, chifukwa iwo akuyankhula mmalirime mokhoza, koma iwo akuchita izo pamaso pa Mulungu. Mwaona? Koma ngati iwo akuyankhula mu malirime ndipo pakakhala pali wotanthauzira, wotanthauzirayo amayenera kuti apereke uthengawo. Mipingo yonse ikubwera ku chimenecho.

114 Charles Fuller, mochuluka momwe iye ankachitira makani ndi kupitiriza pa ine pa izo pamene ine ndinafika uko, iye akuzilandira izo tsopano. Ndipo iwo akuchita izo konse ku Long Beach. Inde, bwana! Mkati momwe—mkati momwe moyankhulira, akumakhala ndi madalitso a Mulungu, kuyankhula mu malirime, kutanthauzira kwa malirime, ndi kumapempherera odwala. Ndipo iye anaima maso ndi maso kwa ine ndipo anati, "M'bale Branham, ine sindikhulupirira mu zinthu zoterozo."

Ine ndinati, "Chabwino, izo ziri kwa inu. Icho si za osakhulupirira, M'bale Fuller, Izo ndi za iwo amene akukhulupirira." Ndipo tsopano iye akulalikira zinthu zomwezo. Zikufika ku nthawi; kuli chiwonetsero.

115 Tsopano ndiye, ngati izo ziri mu dongosolo, ngati izi ziri zomwe inu munali kuzikamba . . . Pamene mlaliki akuyankhula chirichonse chiyenera kukhala chete kuti azimvetsera kwa mlalikiyo. Pakuti apo pali Mawu a Mulungu akuperekedwa, ngati iye akulalikira pansi pa kudzoza. Ndiye, mzimu uliwonse wa aneneri umamvera aneneri. Pamene m'busa ayenda kupita ku nsanja, natembenuza Baibulo ilo apo, mpingo uyenera kuti uzikhala chete, kumamvetsera pa . . . kuwerenga kwake kwa Lemba, kumvetsera chimene iye akuti anene. Ngati iye anena chinachake chimene chikumveka bwino kwa inu, inu mukhoza kunena, "Ameni, Ambuye adalitsike!" kapena chirichonse chimene inu mukufuna. *Ameni* amatanthauza "izo zikhale chomwecho." Baibulo linati tizichita choncho.

116 Ndiye, uthenga ukakhala utatha . . . Ndiye ngati mlaliki apereka malo mmenemo pamene anthu onse akusangalala, Mzimu uli pakati pa anthu, mwina Iye akhoza kutumiza uthenga wina. Ngati Iye atumiza uthenga, iwo ufika kwa winawake, ndiye kutanthauzira; sikukhala . . . kumangonena mobwereza Lemba kapena kumachita chinachake. Mulungu samagwiritsa ntchito kubwereza kopanda pake. Koma iwo uzikhala uthenga wolunjika kwa winawake kuti achite chinthu *chinachake* kapena chinachake chimene chiti chiumangirize Mpingo. Ndiye

pamene iwo alandira kumangiriza kumeneko kwa Mpingo, inu mukuti, inu . . .

117 Monga mwa chitsanzo monga chonchi: Wina ataimirira pano ndi kuyankhula ndi malirime; mmodzi uyu azitanthauzira ndi kuti, "PAKUTI UKUTERO MZIMU WOYERA: Mulole *Wakuti-n-wakuti* apite akaike manja pa munthu uyu cha kuno, PAKUTI UKUTERO MZIMU WOYERA, usikuuno ndi nthawi ya kuchiritsidwa kwawo." Ndi chiani icho?

Ndiye munthu yemweyu akanati, "Ine ndinali nditakhala apo; mtima wanga unali kumangoyakira kwa khanda limenelo." Tsopano—tsopano iwo ayimira mwa kumvera Mzimu, napita kukaika manja pa khandalo, ndipo ilo nkuchira. Ngati ilo silitero, chinachake chalakwika. Mwaona, mwaona? Uwo ndi uthenga wolunjika.

118 Ndiye wosakhulupirira akakhala apo angati, "Dikirani miniti. Ndikuti, Mulungu ali ndi anthu amenewa!" Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

119 Ndiye iye adzati, kapena, "PAKUTI UKUTERO MZIMU WOYERA: Mulole aliyense yemwe ali mmbali ya kummwera kwa mzinda, kuchokera ku mbali iyo ya Spring Street, achokeko mu masiku awiri otsatirawa, pakuti kukubwera nkuntho umene uti udzasese mbali iyo yonse ya mzinda uko nkutha." Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, uwo ndi ulosi wa kwa mpingo wonse.

120 Ndiye winawake—wa kuweruza kwauzimu—aimirire ndi kuti, "Kodi izo zinali za Ambuye?" Aliyense. Ngati amuna abwino atatu aimirira ndi kuti, mwa oweruza auzimu nati, "Izo zinali za Ambuye," ndiye mpingo uchilandire icho; ndipo aliyense wa mbali iyo ya mzinda achokeko, asamukire kutali kwa iyo kwa nthawi imeneyo. Ndiye ngati izo sizifika pochitika inu kulibwino mumufufuze munthu ameneyo. Mwaona? Inu muli ndi mzimu wina pakati panu. Koma ngati izo zifika pochitika, ndiye dalitsani Mulungu ndi kumuthokoza Mulungu pokulolani inu kuti muthawe mkwiyo umene unali kudzawo. Mwaona? Ziziyang'anani zinthu izo. Ndiwo Mpingo uli mu dongosolo.

121 Mauthenga awiri kapena atatu—osati opitirira utatu—uti uzibwerapo pa nthawi imodzi monga choncho. Chirichonse chimene chibwerapo, onani, icho chiyenera kuikidwa mu dongosolo. Malo oyamba . . . ndiye, mpingo wina, chinthu china mu dongosolo . . .

122 Ine sindikudziwa. Uyu akhoza kukhala mkazi yemwe anafunsa izi. Ine basi . . . China chakenso chabwera mu malingaliro anga, kotero ine ndikhoza kungochinena icho. Akazi, pamene iwo ati azibwera mu mpingo, zinali molingana ndi Chipangano Chatsopano, amayenera kuti azilowamo ndi kukhala pansi ndi nkhope yophimbidwa ndi maonekedwe achisoni, ndipo apo azikhala ali ndi msonkhano wonse. Ndizo molingana ndi Lemba. Tsopano. Koma ine ndikuganiza

mkazi . . . Zedi. Tsopano, ine sindiri kukuweruzani inu akazi. Mwaona?

123 Dona wamng'ono anadza kwa ine pakale pang'ono. Osati . . . M'bale Junior anali alipo apo pamene mkaziyo anadza, nati iye anali ndi vuto lina. Oyandikana naye ankamuseka iye, chifukwa iye sakanati amete tsitsi lake lonse kuno osati kale litali. Ndipo iye anapita nakalimetamo tsitsi lakelo. Ndiyeno, mkazi wina patsidya pa mtsinje anasokonezekeratu, ndipo anamuuza iye kuti amati amatenga, njira yauzimu, kuwamanga mapazi ake ndi tsitsi lake—tsitsi, ndipo anamufikitsa mkazi uyu mu mantha. Mkaziyo anali pafupi kuchita misala—wa ana awiri. Iye sanadziwe choti achite. Iye anangokhala apo monga choncho.

124 Iye anayendetsa mpaka kutsogolo kwa nyumba tsiku lina. Mzimu Woyera unasunthira pansi, ndipo unayankhula kwa iye, ndipo unamuuza iye kuti akanati akhale ali bwino, ndi "Ndi PAKUTI WATERO MZIMU . . ." Ndipo iye—iye anakhala monga choncho ndiye kwa masiku angapo, ndiyeno iye . . . Ine ndinapita dzulo, ndimati ndikamuone mkaziyo ndi M'bale Junior ndi M'bale Funk. Ndipo ine ndinali mkati mwa theka la mtunda. Iye anali ataimirira, akupesa tsitsi lake limene iye anali atalileka—atalileka kuti lizikula tsopano, anati, "Asiyeni oyandikana nawo aziseka ndi kuchita chirichonse chimene iwo amachifuna kuchita."

125 Ndiyeno, Mzimu Woyera sukanandilola ine kuti ndipite kumeneko. Ndipo Iwo unayankhula kwa iye ndipo unamuuza iye kuti ine ndinali pafupi ndi kumaloko ndipo ndimafuna kuti ndibwere. Ndipo usiku watha mu masomphenya, ndinamuwona mkaziyo akubwera, ndipo anauzidwa chimene chinali cholakwika ndi iye; ndipo iye anachiritsidwa mu chipinda changa kanthawi kapitako. Mwaona? Nkulondola uko, M'bale Junior? Uko nkulondola. Kanthawi kapitako basi. Mwaona? Mulungu sakanandilola ine kuti ndipite kumeneko chifukwa chinthucho sichinali chitakonzeka apobe. Mwaona? Iye anandibweretsa ine cha pa malo pomwepo ndipo anatsimikizira icho apo pomwe, kuti asonyeze kuti uyo sanali munthu, Uyo anali Mulungu. Mwaona?

Tsopano. Iye anati, "M'bale Branham, mwamuna wanga akufuna kuti ine ndikhale ndi tsitsi lalitali."

126 Ine ndinati, "Mulungu akufuna chinthu chomwecho." Ndiko kulondola, pakuti akazi amayenera kuti azikhala ndi tsitsi lalitali. Ndicho chophimba chawo.

127 Ine ndikudziwa madona ife lero, kapena madona inu, kani, mumavala zipewa. Inu mumati ndicho chophimba chanu. Uko nkulakwitsa. Baibulo linati chophimba cha mkazi ndi tsitsi lake. Ndipo ngati iye alidula tsitsi lake icho ndi chinthu chopeputsa kwa iye kuti apemphere. Nkulondola uko? Ndilo Lemba. Mwaona? Chotero tsopano, akazi amayenera kuti azivala

tsitsi lalitali, mosalabadira za chimene inu mukufuna kuti muziganiza za icho; ndicho chiri PAKUTI ATERO AMBUYE. Inu mungondisonyeza ine malo aliwonse . . .

128 Inu mukuti, "Chabwino, tsitsi langa ndi lalitali. Mwaona, ilo likufika mpaka pa mapewa anga." Ilo ndi tsitsi lalifupi. "Khristu" . . . Inu mukuti, "Khristu anali ndi tsitsi lalitali." Iai, Iye sanali. Khristu anali ndi tsitsi lofika mmapewa, chotero iwo amati. Iwo—iwo amangolikoka ilo mozungulira chotere ndi kulidulapo ilo, tsitsi lofika mmapewa. Kayang'aneni pa mawu Achigriki pa ilo mkati umo, ndipo inu mukazipeza.

129 Tsitsi lachikazi . . . Mwamuna asamakhale ndi tsitsi lalitali, chifukwa izo nzachikazi, kufikira pansi lalitali monga chonchi. Koma Iye ankangolidulira ilo apa pa mapewa Ake, pamene iwo ankalidula ilo, kuzungulira mutu Wake, kungolidula ilo monga choncho. Limenelo linali tsitsi lalifupi.

130 Chotero, madona a tsitsi lofika mmapewa mwawo, ilo likadali tsitsi lalifupi. Tsopano, ine sindikuti izo zingakutengereni inu ku gehena kapena kukutengerani inu Kumwamba. Izo ziribe chochita ndi icho. Koma dongosolo la Mpingo ndi loti akazi azikhala nalo tsitsi lalitali. Ndiko kulondola. Ndi polowa mu mpingo . . . N—ndi kusakhala ndi chirichonse chochita mu zochitika, zochitika zachisangalatso—kapena osati ku—ine ndikutanthauza zochitika mwantchito ya mpingo. Ndipo iye ndi woti azikhala womvera, ndi wolemekeza, ndi zina zotero monga choncho, chifukwa iye anali, Baibulo linati, yemwe anabweretsa kugwa koyamba. Ndipo uko nkulondola; nkulondola. Tsopano, mofulumira kumene. Ine ndikuyembekeza izo sizinapweteke.

19. Funso: **Chifukwa chiani masomphenya a Mulungu anabwera patsogolo panga pamene ine ndinali pafupi kutenga Mgonero ku mpingo wanga? Latha.** (Chabwino, ilo ndi dzina la mkazi chabe; inde, ilo ndi dzina la mkazi,) **C . . . Chifukwa chiani masomphenya a Mulungu anabwera patsogolo pa ine pamene ine ndinali pafupi kutenga Mgonero ku mpingo wanga?**

131 Chabwino, ine sindingadziwe, Mlongo, pokha ngati icho chinali ichi: Ngati inu munaona Yesu Khristu ataonekera mu masomphenya ku mpingo wanu pamene inu munali kutenga Mgonero, Iye anali kukulolani inu kuti mudziwe ichi: kuti inu munali kumutenga Iye mwa chophiphiritsa. Mgonero ndi woti uziimira thupi la Yesu Khristu; ndipo inu munali kumutenga Iye monga chophiphiritsa kumulowetsa mu thupi lanu. Chotero zikhalani mwachiyero, ndi kumakhala mwangwiro.

132 Mvetserani. Ngati inu mutenga Mgonero (inu muzimva izo zikuwerengedwa basi mu maminiti pang'ono) pamene inu muli wosayenera, ndinu ochimwira Magazi ndi Thupi la Yesu Khristu. Munthu azitengera gulu limenelo moyenera pamaso pa Mulungu,

yemwe amatenga Mgonero uwo, kani, azikhala moyenera pamaso pa Mulungu. Musati muziutenga iwo mosayenera. Ndiko basi . . .

133 Penyani. Baibulo linaneneratu mu masiku otsiriza kuti magome onse a Mulungu akadadzakhala odzaza masanzi. Ndipo sipakadadzakhala wina wokhoza kuti—kuti amvetse. Nkulondola uko? Penyani. Ine ndinapita osati kale litali mu kachisi wamkulu. Ine sindingatchule dzinalo; inu nonse mukukudziwa uko bwinobwino. Inu mukudziwa chimene iwo anali nacho cha mgonero? Iwo anatenga mtanda wa mkate, mkate wamoyo, mkate wopepuka, ndipo anaudula iwo. Ndipo gulu la madikoni, amene mlalikiyo anati seveni a iwo anali zidakhwa . . . Ndiko kulondola. Ndipo aliyense wa iwo, gulu lonselo . . . Inu mukanakhoza kuwaona iwo pamene iwo ankapita kudutsa mu chinyumbacho akuyankhula kwa anthu. Ndipo pamene mpingo unabalalitsidwa, pa mapeto, pakati pa Sande sukulu ndi mpingo, pafupifupi mmodzi aliyense, m'busa ndi onse, anatuluka ndipo ankakasuta ndudu panja, ndipo anabwerera mkati ndi kumadzatenga Mgonero wa Ambuye. Mulungu ananena kuti Iye sakanati adzakugwireni inu wosalakwa pa izo. "Ndipo ambiri akudwala ndi kufooka pakati panu, ndipo ambiri ali kufa." Ndiko kulondola.

134 Anati, "Magome onse a Mulungu ali odzaza ndi masanzi, ndi ndani yemwe Ine ndingakhoze kumuphunzitsa chiphunzitso." Iye anati, "Pakuti gawo liyenera lizikhala pa gawo, mzere pa mzere, ndi pano pang'ono ndi apo pang'ono. Gwiritsitsani zolimba ku chimene chiri chabwino. Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena Ine ndidzayankhula kwa anthu awa, ndipo uwu ndiwo mpumulo umene ine ndinati ukanadzakhala ulipo kuno, koma ndi izi zonse iwo akanamadzagwedeza mitu yawo ndi kuyenda kuchokapo ndi kuti, 'Ife sitizimva izo.'" Penyani pamene ife tiri kukhala, abwenzi. O, chifundo! Galamukani!

135 Inde, masomphenya anu, Mlongo . . . Ngati inu muli mkazi wabwino, woyera, wopatulika pamaso pa Mulungu, inu munali kuima apo ndipo Yesu anali kukupangitsani inu kuti mudziwe kuti Iye anali kupereka Mgonero, kuti inu munali kumutengera Iye mkatimo ngati chophiphiritsa; ndipo ngati inu simuli, ngati chenjezo kwa inu kuti mukhale bwino ndi Mulungu inu musanazichite izo kachiwiri.

20. Ine ndikanafuna ndidziwe chimene l—lotsatirali liri: 1 Timoteo, wa 2—ll Timoteo mutu wa 2 ndi ndime ya 16.

136 Mphindi yokha. ll Timoteo . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] Ife timabwera palimodzi. Mwina inu simugwirizana ndi chimene ine ndinanena. Zitengereni inu kunyumba . . . Ndiye, inu mupite kunyumba ndi kukawerenga mochuluka kwambiri, ndiyeno izo zikukuthandizani inu

kuti mukhale auzimu. Chabwino, ll Timoteo 2 ndipo 16 akuwerengeka monga chonchi:

> *Koma pewani zotukwana ndi zoyankhula zopanda pake: pakuti izo zidzachulukitsa ku kupanda umulungu kochuluka*.
>
> Inde. **Chabwino, inu mukufuna kuti mudziwe chimene "kuyankhula zotukwana" chiri. "Zotukwana . . . pewa kubwebweta zotukwana, pakuti izo zichulukira."**

137 Tsopano, chinthu choyamba ndicho, "kubwebweta zotukwana, pakuti izo zidzachulukira." Tsopano, chirichonse chimene chiri basi chokalamba—chimangopitirira kubwebweta. Baibulo linati—Yesu anati, "Mulole 'inde' wanu akhale 'inde' ndi 'ayi' wanu akhale 'ayi' pakuti chirichonse chochulukira kuposa ichi chitembenukira ku tchimo." Inu simukuyenera ngakhale kuchita nthabwala ndi kunenana wina ndi mzake. Mulungu adzakupangitsani inu kuti mupereke choyankha chifukwa cha liwu lirilonse lopanda pake limene inu muliyankhula. Inu mukuzidziwa izo? Baibulo linanena kuti inu mudzayenera kupereka choyankhira pa liwu lirilonse lopanda pake. Chotero ndi anthu a mtundu wanji omwe ife tikuyenera kuti tikhale? Anthu amene ali owonamtima, olimba, okonda, achifundo, ndipo osati ochuluka zamkutu, nthawi zonse kumapitirira . . .

138 Penyani. Inu mutenge munthu yemwe angayambe lero . . . Ine ndachizindikirapo icho pa inemwini, ndipo pokhala wa chibadwa changa chomwechi, munthu wa Chiairishi; ine ndakhala nthawizonse ndi mphepo yambiri pa ine mulimonse, kuduliza ena ndi kumangopitiriza. Ndipo monse—muli monse kawirikawiri ngakhale mkazi wanga amati, "Tsopano, Bill . . . !"

Ine ndimati, "Uko nkulondola, Wokondedwa." Iye amati, ine ndikuwakankha ana . . . Ine ndikati . . . Kuwaduliza iwo kapena chinachake, nkuti, "Chabwino tsopano, inu mukudziwa, panali amuna aakulu atatu amene anabwera kuchokera mu Kentucky."

"Anali ndani awo?"

"Chabwino, Abraham Lincoln."

"Eya."

"Daniel Boone."

"U nhu."

"Ndi abambo anu." Chinachake monga choncho.

139 Ndipo iye amati, "Tsopano, Bill, apo iwe ukupita nazo kachiwiri." Ndipo ine ndimachita kupita kokadzitsekera kwinakwake, ndi kukati, "Ambuye, mundikhululukire ine, ine sindimatanthauza kuti ndinene izo. Chitani chinachake kwa ine; ndipangitseni ine kuzisiya izo." Mwaona?

140 Ndipo tsiku lirilonse ine—ngati ine ndichita izo . . . Tsopano, ife tinali kuyankhula pa liwu la *kubwerera mmbuyo* mmawa

uwu. Pamene inu muchita izo inu mwabwerera mmbuyo. Inde, bwana! Inu muyenera kuti mulape. Nkulondola uko? Tsopano, ine sindikutanthauza kuti inu munapita kunja mdziko ndipo inu munakachita *izi* ndi *izo*, koma inu mwachita chinachake. Inu mumayenera kuti muzilapa ndi kumafa patsiku kuti muzikhala mwa Yesu Khristu. Chotero lirilonse, tsikundi tiiku, tsiku lirilonse, inu mumayenera kuti muzifa tsiku lirilonse kuti muzikhala moyo mwa Khristu Yesu.

141 Pamene ine ndichita chinachake . . . Nthawi zambiri ine ndimachita zinthu zimene ziri zolakwika. Ine ndimakhala kunja, ndipo winawake nkunena chinachake kapena chimzake, ine mwina ndimakhoza kunena kanthabwala kochepa pa izo. Winawake nkunena . . . Osati ili yoipa; tsopano, ine sindikhulupirira kuti Akhristu amanena nthabwala zonyansa. Iai, bwana! Iai, bwana! Izo siziri ngakhale zoyenera kwa Akhristu, Baibulo linatero. Ilo linati kanani zinthu zakale zotukwana zonga izo, ndi nthabwala, ndi kukankhana, ndi zinthu zonga izo. Ayi, Akhristu samanena zinthu zimenezo; Akhristu ali ndi maganizo angwiro.

142 Koma ngati inu simusamalira, kamodzi mu kanthawi inu muzikhala naye munthu . . . Iye azinena kanthabwala kakang'ono lero. Ndipo chabwino, Iye angoganiza kuti izo nzabwino, ndipo iye nangozileka izo zipite motero, ndi kusaganiziraponso nkomwe za izo ayi. Tsiku lotsatira iwe unena tinthabwala tiwiri tating'ono. Mwaona? Ndipo chinthu chotsatira inu mukudziwa, inu mukuchita chinthu chinachakenso. Ndipo chinthu choyamba chomwe muti mudziwe, icho chimangotsogolera kubwerera mmbuyo ku kachitidwe kachikale komwe kaja kachiwiri. Nkulondola uko? Khalani kutali ndi zinthuzo. Zipeweni izo! Ndipo pewani kubwebweta motukwana uko.

143 Inu munamva . . . Wina kubwera uko . . . Ine ndingokupatsani inu chitsanzo chaching'ono. "Akazi a Doe, kodi inu mukudziwa chiani? Ine ndinawaona amuna anu. Ndipo ine ndikuuzeni inu chiani. Ndipo iyendi dikoni." Mwaona? Pamene . . .

Tsopano, ine ndikungoganiza . . . Nenani, "Ine sindikufuna kuti ndizimve izo!" Nkulondola uko, ndipo kaziyendanibe. Osamatenga zambiri za izo, ndipo iwo adzazilekeza izo. Uko nkulondola.

144 "O, inu mukudziwa chiani, Mlongo? Ine ndikuuzeni inu chimene chinachitika kwa M'bale." Osati mlongo yekhayo, koma m'bale nayenso. Mwaona?

"M'bale, ine ndikuuzani inu chimene chinachitika. Inu mukudziwa ife tikanangomuchotsa mlaliki uyu, ife tikanachita *izi*, kapena kumuchotsa dikoni uyu, kapena ngati ife tikanachita *izi*." O, o! Ingo—ingo—ingozipewani zinthu zimenezo.

145 Ine ndikuganiza kanthu kabwino kakang'ono komwe mukanayenera kuti muzikaika powonekera pa desiki panu, ndi kanthu kakang'ono kamene ine ndinakaona uko ku Florida osati kale litali. Iwo anali ankhwere aang'ono atatu; ndipo kamodzi ka ito kanali ndi timanja take pa timaso take, ndi kumati, "Osamaona choipa ayi"; ndipo kamodzi kenako kanali ndi tizala take mu timakutu take, ndi kumati, "Osamamva choipa ayi"; ndipo kamodzi kenako kanali ndi kadzanja kake pa kamwa kake, iko kamati, "Osayankhula choipa ayi." Ine ndikuganiza icho ndi chinthu chabwino sichoncho inu? Inde, bwana! O, mai! Icho ndi chinthu chabwino kwambiri.

146 Ingosungani malingaliro anu mwangwiro ndi pa Khristu. Inu simungangoti, "Chabwino, tsopano . . ." Tsopano onani, ngati inu simusamalira, inu mudzipeza nokha mpaka pa malo, ngati inu mupitirira kumaganizira izo . . . Inu simuli—ndipo musati muziganiza kuti . . . Inu simungakhoze kumakhala mwangwiro kwambiri mpaka kuti inu simungapange cholakwitsa icho tsopano. Tsopano, inu musati muziganiza kuti inu mudzakhala konse mwanjira yoteroyo, chifukwa inu simudzatero. Ayi, bwana! Inu simuli wopanda tchimo, ndipo ndithudi inu mudzachoka pa njirayo, ku mbali iyi ndi ku mbali iyo.

147 Koma munthu yemwe anagwetsedwapo kamodzi pansi, ngati iye ali msirikali weniweni iye amaukapo kachiwiri. "Ambuye, ndiroleni ine ndiuke ndi kuyeseranso icho kachiwiri." Koma wamantha, mwamsanga pamene iye awona kuti iye wapanga cholakwitsa chake choyamba chaching'ono, monga ine ndinanena mmawa uwu: gonondo ndi kangaude wammadzi amakwawira mmbuyo momwe kubwerera mmadzi kachiwiri. Mwaona? Iye sangakhoze basi kupirira nazo izo.

148 Chotero kanani zonse zakale—kubwebweta zotukwana uko kupitiriza, kuyankhula. *Kubwebweta* kumatanthauza "zosokonezeka." Ndipo Baibulo linati. "Adziweni awo amene amayambitsa mikangano pakati panu."

149 Ngati wina anena, "U-nhu! U-nhu," tsopano basi—tingoti, "Inu muli bwanji? Ine ndiri wokondwa kukuonani inu kachiwiri. Zikomo." Ndipo zingomapitirirani. Ndicho chinthu chopambana. Musati muziwapewa iwo, koma muzingowadziwa iwo musati muzipereka chidwi chirichonse, chifukwa inu mukuona kumene izo zimalondolera.

21. Anali kuti Yesu kuchokera Kwake—Kodi Yesu anali ali kuti kuchokera pa ubatizo Wake mpaka pa zaka zitatu za utumiki Wake?

150 Chabwino. Yesu, pamene Iye anabatizidwa, anapita molunjika natuluka mmadzi, ndipo Mzimu unamutsogolera Iye kumka ku chipululu kwa masiku forte, ndi mausiku kuti akayesedwe ndi mdierekezi. Ndipo Iye anayesedwa masiku forte ndi mausiku. Ndipo Iye anasala. Iye anabwererako.

Mdierekezi anamuyesa Iye pamene Iye anabwererako kutatha kusala Kwake. Ndipo Iye ankamukaniza mdierekezi ndi Mawu a Mulungu, ndipo analowa mu utumiki Wake, ndipo analalikira zaka zitatu ndi theka, molingana ndi Malemba.

151 Penyani. Kutali mmbuyo uko mwa Daniele Mulungu anayankhula ndipo anati Iye akanadzalalikira zaka zitatu ndi theka ndi kuti adzadulidwapo kuti akhale nsembe mu nthawi imeneyo. Ndendende basi. Kumaziko a dziko lapansi Iye anali atadzozedweratu. Ndiko kulondola.

152 Mateyu mutu wa 4, inu mukazipeza izo. Ngati icho sichiri ndendende basi molingana ndi chikhulupiriro chanu, chabwino.

Tsopano, limodzi ilo ine sindiri . . . Tiyeni ife tione chimene . . . O, inde. "Alikuti a . . . ?" Ife tinali nalo ilo kanthawi kapitako. "Alikuti akufa?"

22. Pa nthawi imodzi—pa nthawi imodzi kodi ife tonse tinali oyera kapena achikuda? Mwa awiriwa, ndi pa uti amene themberero linaikidwapo?

153 Tsopano, monga momwe ife tikudziwira, ine sindikanakhoza kukuuzani inu ngati Adamu ndi Eva anali—anali oyera, kapena abulauni, kapena achikasu, kapena okuda. Ine sindingakhoze kukuuzani inu. Palibe mmodzi wina akudziwa koma Mulungu yekha, ine ndikuganiza; Iye analipo mmbuyomo uko. Tsopano, mu m . . . Momwe ife tinadzera tonse monga a chinenero chimodzi ndi anthu amodzi mpaka ku nsanja ya Babulo, chisokonezo. Ndiyeno zinenero zawo zinapita mosiyana. Ndipo momwe ife tikudziwira iwo anali onse anthu amodzi mpaka nthawi imeneyo. Ndipo iwo anagawikana ndipo anabalalikira mu magawo osiyana a dziko.

154 Ndipo ena . . . Inu mukatenga chinyama; inu mutenge moyo uliwonse umene umadya kuchokera mu dothi linalake, iyo imasandulika mtundu umenewo. Ngati muli osaka muno, inu mungonditsata ine maminiti ochepa. Pitani kumusiko mu Mexico, ndipo mukaipeze nkhandwe; tengani kuno mu Arizona ndipo mukaipeze nkhandwe; inu mupite Kumpoto uko ndi kukapeza nkhandwe yomweyo, ndipo muone mitundu itatuyo. Mukatenge mng'azi amene wakulira mu Texas, ndi kukatenga wina amene wakulira mu Arizona, ndipo muyang'ane pa kusiyanako pa iwo (mwaona?), chifukwa ndi dothi lomwe iwo amakhalanalo moyo. Mwaona?

155 Ndipo tsopano, Wachichaina, Wachichaina ndi—munthu wachikasu, wachi Japan, ndi ena otero, ndi Wachichaina. Wachi Ethiopia ndi—ndi munthu wachikuda, kapena Mnegro yemwe ife tiri naye tsopano. Ndipo iye anapita kumusi uko mu maiko okuda awo kumusi uko.

156 Ndipo iwo—ndi—ndipo iwo anali . . . Ndiyeno anthu oyera anali anthu achi Anglo-Saxon omwe ife tiri. Ndipo, ka—ka anthu kuno, amene ife timawatcha anthu oyera, iwo anabwera

kuchokera ku England komwe kale kunkatchedwa "dziko la Angelo." Ndipo chifukwa iwo anali oyera, ndi tsitsi lofiira, ndi zina zotero . . . Ndipo anabalalikira mpaka ku Ireland, ndi Norway, ndi kwina kotero—mpaka uko. Ndipo iwo onse anabwera kuchokera mwa anthu achi Anglo-Saxon.

157 Tsopano, ndi uti anali woyamba ndi amene anatembereredwa? Panalibe mmodzi wa iwo. Ine ndikudziwa kumene inu mukuyesera kupita. Inu mukuyesera kuti mufike kwa Hamu. Ine ndikudziwa kumene inu mukupita—kwa anthu a Hamu.

158 Tsopano, panali Hamu, Semu ndi Yafeti. Tsopano Hamu, i—i—iye sanayesere kubisa umaliseche wa abambo ake ayi, koma anawaseka ndi kumawanyazitsa iwo. Ndipo Mulungu anaika themberero pa Hamu chifukwa choyang'ana pa umaliseche wa abambo ake ndi kusayesera kuwaphimba manyazi awo. Ndipo Semu ndi Yafete anayenda chammbuyo ndipo anaponyera zikhoto zawo pa atate awo pamene iye anali atagona mbulanda. Ndipo tsopano, Mulungu anamuuza Hamu kuti m'badwo wake ukadadzamawatumikira enawo.

159 Tsopano, ngati inu mumaganiza kuti ilo linali themberero, kukhala wakuda, chabwino ndiye, Myuda ndi wakuda nayenso. Ngati inu mukuganiza kuti awo akanakhala a—a—amene ife timawatcha anthu achikuda kapena Anegro a mdziko lino amene ali kuno tsopano, inu muyenera kuti mupite uko ku India. Amwenye ndi oderapo kwambiri kuposa Achinegro. Ine ndapitamo mu maiko a onsewo. Apa pali uyu wa—wachi Ethiopia kumusi uko wochokera ku Ethiopia, ndi wachi Afrika, munthu wachikuda yemwe ife tikumudziwa lero. Iwo ali kumusi uko, ambiri a iwo akadali mu kupulikira, mu mafuko awo. Basi monga ife tinaliri pamene Yesu anabwera.

160 Anthu oyera anali opulikira basi monga m—mbadwa za ku Afrika ziri tsopano, moipirapo mwina. Kumbukirani, zaka thuu sauzande zapitazo ife tinali mtundu wa anthu osavala kunja uko ndi—tiri ndi uta ndi muvi ndi nkhwanga ya mwala, yosakira (uko nkulondola ndendende), ife anthu achi Anglo-Saxon. Uko nkulondola ndendende. Chotero ndi uti amene anali uti?

161 Ine ndikuuzani inu mmodzi yemwe lero ali wotembereredwa ndi uyo amene amamukana Yesu Khristu. Ndizo zonse. Uyo yemwe amamulandira Yesu Khristu ndiye wodalitsidwa.

162 Tsopano, inu simungakhoze kunena . . . Ine ndikapita uko, kukamtenga wachi Eskimo, kuchokera ku dziko ilo kutali uko. Ndipo kumeneko iye ali kumtunda uko; ndipo munthu uyo ndi woderapo kuposa anthu achikuda omwe ife tiri nawo kuno. Ine ndikapita ku India ndi kukawatenga Amwenye; ndipo iye ali—iye si munthu wachikuda, iye ndi wakuda kweni kweni. Iye ndi woderapo kuposa—mtundu weniweni wakuda. Ndipo chimene iye ali ndi chomwe chimatchedwa . . . Ndipo iye ndi mmwenye.

Chabwino tsopano, mu Afrika ife timawapeza anthu ena achi Afrika amene ali . . . Ena a iwo ndi oyezukirapo; ena a iwo ali pafupi ngati oyera; ndipo ena a iwo ndi—ali mwa njira zosiyana.

163 Inu mukapita kwa Ayuda; ndipo inu mukati Ayuda onse ndi—a maonekedwe okuda. Myuda ndi munthu wa bulauni, koma ine ndawonapo ena ambiri a mutu-wofiira ndi maso a buluu, khungu losalala. Mwaona?

164 Chotero chinthu chonsechi ndi izi: ife tonse tabwera kuchokera ku mtengo umodzi. Ndiko kulondola. Ndipo ife tonse tinatembereredwa kupyolera mukugwa kwa mu Edeni. Ndipo ife tonse tinapulumutsidwa kupyolera mu chiukitsiro cha Yesu Khristu. Ndi izo apo. Chotero palibe themberero. Otembereredwa ndi iwo amene samakhulupirira, koma odalitsidwa ndi iwo amene amakhulupirira. Chotero palibe ngakhale mmodzi, bwenzi, wakuda kapena munthu wachikuda, kapena munthu woyera kapena munthu wachikasu. Ndiye, ngati munthu wakuda akanakhala wotembereredwa pa kukhala wakuda, ndiye munthu wachikasu ndi wotembereredwa mwatheka mokha. Ndiyeno—ndiyeno munthu wachikasu—ndiyeno munthu wa bulauni, iye ali basi mwa magawo awiri pa atatu a njirayo wotembereredwa. Mwaona? Ndiyeno, wa ku Afrika ali pafupi magawo anai pa asanu wotembereredwa. Ndipo ine ndikuganiza Mmwenye ndi wotembereredwa kwenikweni ndiye. O, mai! Zamkhutu bwanji! Iai! Ndi kusiyana kwa malo ndi zinthu zomwe anthu amakhalamo. Iwo anasandulika, anwintha mtundu ndi zina zotero, iwo anali osiyana.

165 Tayang'anani pa Mmwenye wa Chimereka. Ambiri a iwo . . . Anavaho kunja uko ndi mtundu woderapo wa anthu kuposa anthu athu aku Ethiopia mu dziko lino, Anavajo. Apache ali . . . Iwo ali mwa mtundu wa b—mtundu wa kopala. Ndi mitundu yosiyana . . . Mwaona? Kotero komweko pakati pa Amwenye, komwe kuno, inu mumawapeza okudawo, ndi pafupi . . . Ndipo Acherokee ali pafupi otumbululuka monga ife tiri, Acherokee. Ndipo alipo mommuno mu dziko lino, mitundu yosiyana. Chotero inu mukuona, inu simungakhoze kunena kuti iwo ali otembereredwa mwa theka ndi otembereredwa njira yonse. Iwo sanatembereredwe chifukwa iwo anali akuda. Iwo sanatembereredwe chifukwa iwo anali achikasu kapena chifukwa iwo anali oyera. Pali themberero limodzi lokha limene ine ndikulidziwa, ndilo kusakhulupirira pa Yesu Khristu. (Ine ndikudziwa, Donny, ino ndi nthawi yoti ine nditseke, koma ine ndiri nao mafunso awiri owonjezerapo.)

23. Chabwino tsopano. **Alikuti mafuko omwazikana khumi a Israeli otayika (Genesis 44:49), fuko la Yosefe ku mafuko ambiriwo? Simeoni, Levi, amene anali wopanda dziko lakwao lao lao, koma ali omwazikana pakati pa mafuko ena**

khumi . . . Ali kuti mafuko khumiwo? Kodi ife tingakhoze kuwapeza iwo?

166 Inde, bwana! Iwo akhoza kupezedwa. Mwapamalo iwo akhoza kupezedwa mu Baibulo. Ndipo Mulungu amatiuza ife uko komwe iwo ati adzakakhale ali mu masiku otsiriza ndi chomwe chiti chidzakhale chitsiriziro chawo. Ndipo pakali pano, ine ndinangowerenga bukhu, limene uko mu Israeli kumene iwo anali, kumene iye ananena kuti mmodzi anaviika phazi lake mu mafuta ndi chirichonse. Mulungu ali nawo onse ataikidwa mmalo awo, atakhazikitsidwa mmalo osiyana. Ndipo Ayuda onse akubwerera ku Palestina, kumene Mulungu analonjeza mu masiku otsiriza kuti iwo adzakakhala ali kumeneko.

24. Funso limodzi loonjezera: **Ndingakhoze—ine sindingakhoze kukhulupirira kuti Mulungu anatumiza nkhondo ngati chiweruzo. Ine sindingakhoze kukhulupirira kuti Mulungu amatumiza nkhondo ngati chiweruzo.** (Tangomvetserani kamphindi.) **Ine sindikhulupirira, monga ena amachitira, kuti Mulungu amaika lupanga mmanja a okupha awa kuchokera ku Babeloni wamakezana mpaka kwa Hitler, kuti azipha akazi ndi ana osalakwa palimodzi ndi—palimodzi ndi olakwa, kuti achite chiweruzo cha Mulungu. Asati Mulungu—Mulungu wanga wa chikondi sakanakhoza kuchita—Mulungu wanga wa chikondi** (Ndikhululukireni ine!)—**kuchita ichi. Nkhondo ndi ntchito za Satana. Chonde tsimikizirani chisokonezo ichi.**

167 Tsopano, mphindi yokha. Ine ndinaliwerenga ili kanthawi kokha kapitako, chifukwa chomwe ine ndinaliikira ili pansi. Tsopano, ine ndikufuna inu kuti mungogwira bata lanu miniti. Tsopano, tiyeni—tiyeni ife tizitenge izi moongoka kwenikweni, chifukwa ili ndi funso ndithu. Ndipo ilo liyenera kuyandikiridwa molemekeza. Mwamsanga likangotha ilo, ngati inu mungakhoze kupirira nafe motalikitsa pang'ono pokha . . .

168 Ine ndikudziwa tikuyamba kuchedwa, koma ndi chiri . . . Kumbukirani, nchiani pa izo? Tsopano, inu munkakonda kupita kukavina usiku wonse ndi kusaganiza kanthu za izo (mwaona?), kukakhala kunja pa zinthu zachidziko, koma pamene zifika ku Mawu a Mulungu kupitirira maminiti makumi awiri, m'bale, ife tiyenera kuti tipeze mlaliki watsopano. Mwaona? Izo nzamanyazi. Paulo analalikira usiku wonse. Ine ndinkalalikira pomwe pano zaka zapitazo pa 2 ndi 3 koloko mmawa. Ndipo anthu kumakhala akuyenda chobwera ndi kuchokera ku malo awa muno akungoyamika Mulungu nthawi ya 2 koloko kapena 3 koloko mmawa. Inu mumakhoza kuwaona ochuluka kukwana khumi ndi awiri mwakamodzi akulandira Mzimu Woyera nthawi ya 2 ndi 3 koloko. Mulungu atichitire chifundo. Ine ndikukhumba ine ndikanazionanso izo kachiwiri. Koma ife sitingakhoze; tsiku lapita. Tsikulo lapita tsopano; ilo latsirizidwa patali tsopano. Usiku ukuyandikira pafupi ndipo

anthu ali. . . "Chabwino, ife sitikusamalanso basi, chotero. . . Mai, ine ndikukhumba iwo akadasiya, kuti ife tizikonzekera zokalowa mkatimo." Ndi momwe—ziri pafupi basi momwe izo zikupitira.

169 Dikirani, ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake tsopano. Tsopano, ine ndikuti ndisagwirizane nanu, M'bale kapena Mlongo, ine sindikudziwa. Ilo linaikidwa pano mmawa uno. Ine ndinali nalo mu Baibulo langa ndipo ndinali kuyang'ana pa ilo kanthawi kapitako. Tsopano, mwa njira yaubwanawe. . . Ndipo tsopano, ine sindikufuna kuti inu—kuti—kuti muchitire ukali pa ine. Ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwatcheru.

170 Ndipo kumbukirani, ine ndikanati mochulukira monga momwe ndikanakondera kuti ndivomerezane nanu inu pa ichi—pa lingaliro lanu pa ichi monga ine ndinachitira ndi mkazi ujayo, mkazi wosauka kanthawi kapitako. Anati. . . Iye ndi mwamuna wake, iwo anangofulumira ndipo anakwatirana; ndipo apo izo zinali. Koma iye anatenga lumbiriro lake; inu muyenera kuti mumamatirane nalo. Mwaona? Ndipo tsopano, ine ndiyenera kuti ndimamatirane nao Mawu a Mulungu.

171 Koma tsopano, "Ine sindikukhulupirira. . ." Koma choyamba, "Ine sindingakhoze kukhulupirira kuti Mulungu amatumiza nkhondo ngati chiweruzo." Chabwino tsopano, mzanga, pali chinthu chimodzi chokha chimene chiri cholakwika ndi chikhulupiriro chanu, ndipo icho ndicho, izo siziri Mwamalemba. Mulungu amatumiza nkhondo ngati chiweruzo. Ndiko kulondola. Ine—ine ndikupatsani inu Lemba; ine sikuti ndingoliwerenga ilo pano ndiye nkukuuzani inu.

172 Penyani. "Ine sindimakhulupirira monga ena amachitira kuti Mulungu anaika lupanga mmanja a okupha awa ochokera ku Babeloni wamakedzana mpaka kwa Hitler, kuti azipha akazi osalakwa ndi ana." Ngati ine ndikanati ndikuuzeni inu mu Dzina la Yesu Khristu kuti Iye ankachita ndithu izo, ndi kuzitsimikizira izo mwa Baibulo, kodi inu mukanati mukhulupirire izo ndiye (mwaona?), kuti Iye ankazichita izo, kapena—ndipo Iye adzazichita izo kachiwiri? Chabwino. Mvetserani kwa izi.

173 Ine sindikudziwa. Uyu akhoza kukhala bwenzi langa lapachifuwa wakhala muno mwa onse amene ine ndikuwadziwa; pakuti Mulungu yemwe ali Kumwamba akudziwa kuti ine sindikudziwa nkomwe malembedwewa. Ine sindikanakhoza kukudziwani inu. Koma ine ndikufuna kuti inu mumvetsetse ichi. "Mulungu wanga ndi Mulungu wa chikondi—Mulungu wanga ndi chikondi ndipo sakanakhoza kuchita izi. Nkhondo ndi za Satana." Ine ndigwirizana nanu kuti nkhondo ndi za Satana. Izo ziri ndendende. Iye ndi kalonga wa mdziko umu. Ufumu uliwonse ndi fuko lirilonse mu dziko umu mwiniwake ndi Satana. Mulungu anati iwo ali mu Mawu Ake. Satana

anati, “Iwo ndi anga.” Yesu anavomereza kuti iwo anali ake. Koma Iye akhala wolandira onse awo pakapita kanthawi, Yesu adzatero. Ife sitidzakhala ndi nkhondo zinanso apo. Koma Mulungu amamuloleza Satana kuti azichita izi pofuna kukonza ndi pofuna kuweruza

174 Tsopano, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake basi ife tisanayambe. Ine ndikufuna kuti inu mundiyankhe ine ichi ndi kuchipeza. Ngati inu simukukhulupirira kuti Mulungu ali . . . (Inu munati) . . . kuti sakanamachita zinthu zimenezi. Kungoti tichiyambire icho kumene kuchokera koyambirirako . . . Tsopano, ndipatseni ine tcheru chanu kosagawanika ngati inu mungathe. Mvetserani. Nchifukwa chiani Mulungu Mwiniwake anamukwapula Mwana Wake yemwe ndi kumuphera Iye pa mtanda? Mulungu anamupha Mwana Wake yemwe pa mtanda. “Komabe icho chinamukondweretsa Mulungu,” linatero Lemba, “kuti amukanthe Iye, ndi kumutunduza Iye, ndi kumuvulaza Iye.” Mulungu anamuchitira Mwana Wake yemwe motero kuti akupulumutseni inu.

175 Ine ndikufuna kuti ndikufunseni za Sauli, mfumu yaikulu ya Israeli. Mulungu anamuuza iye kuti apite uko ndi kukamutenga mfumu Ogi ndi chirichonse iye anali nacho ndi kuononga kwathunthu chirichonse kumeneko, amuna akazi, ana, ndi chirichonse . . . Ndipo Sauli . . . ngakhale ng’ombe kuti aziphe izo, osati aleke chinthu kuti chikhale ndi moyo. Ndipo Sauli anapita uko ndipo analeka zina mwa ng’ombezo. Ndipo Mulungu anauchotsa Mzimu pa iye ndipo anamulekanitsa iye kwa Iye; iye anakhala mdani wa Mulungu.

176 Chifukwa chiani Eliya anaima paja pamene Mulungu anapereka mfumu Ogi yokalambayo mu—manja a Ahabu? Ndipo iye anamuuza Ahabu kuti aiphe mfumu imeneyo. Ndipo Ahabu anakana kuchita izo. Ndipo Eliya mneneri anali ndi womthandiza kuti . . . Anati, “Ndikanthe ine ndi lupanga lako.” Iye anazindikira kuti iye anali mneneri.

Iye anati, “Ine sinditero.” Ndipo iye anataya moyo wake. Ndiye iye anamuuza mmodzi wina, anati, “Ndikanthe ine.” Ndipo mwamunayo anamumenya iye ndi lupanga ndipo anamuchokera iye. Ndipo iye anadzikulunga yekha modzizimbayitsa ndipo anaimirira apo. Ndipo apa panadza Ahabu atakwera pa gareta wake.

Iye anati, “Nchiani—iwe waimira chiani pano?”

Iye anati, “Chabwino, ine ndinali wolondera; ine ndinapatsidwa usamaliro pa mwamuna. Ndipo iye anandikantha ine ndipo wathawa,” Iye anati, “ndipo ine ndamulola iye apite. Ndipo iwo andiuza ine kuti ngati ine ndatero, ine ndiyenera kuti ndilipire ndi moyo wanga womwe.”

Iye anati, "Chabwino, iwe uyenera kuti ulipire ndi moyo wako womwe."

Iye anadzivundula yekha ndipo anati, "PAKUTI ATERO AMBUYE, chifukwa iwe sunamuphe mfumu ija kumusi uko, iwe ulipira izo ndi iwemwini." Nkulondola uko? Ndiko kulondola ndendende.

177 Ndiroleni ine ndikuwerengereni inu chinachake pano. Nanga bwanji Babeloni, pamene Yoswa—pamene Mulungu anatumiza Yoswa uko kuoloka apo, ndipo iye anawononga kotheratu makanda, ana, ndi china chirichonse. Ndipo ngati iye akanalola chinthu chimodzi chikhale moyo. . . Iye anaseseratu chirichonse uko. Makanda ang'ono Achifilisiti, iye anangowaonongeratu iwo. Mulungu anamulamulira iye. Ndipo ngati iye akanati asachite izo, iwo unali moyo wake womwe.

178 Ine ndizikonza izo mu maminiti ochepa. Mulungu ndi chikondi, chikondi changwiro; koma inu simukudziwa chimene chikondi chiri. Ndi chifukwa chake lero anthu sakudziwa chomwe chikhulupiriro chiri. Mulungu ndi chikondi. Iye ayenera kuti azikhala mu chikondi; Iye ndi wochitamwayekha kwa Mawu Ake. Ndipo Iye ayenera kumasunga Mawu Ake. Iye ayenera kumakukondani inu. Ndipo ngati Iye amakukondani inu, Iye ayenera kuti azikutetezani inu.

179 Mvetserani pano. Inu mukanena za kugwa kwa ana. Miniti yokha, ndiroleni ine ndikuonetseni inu chinachake pano mu Malemba, chi—chimene Baibulo limanena za zinthu izi apa. Tiyeni ife tifike cha apa ndipo tingomvetsera kwa izi miniti yokha ndipo tiwone chomwe Mulungu ananena. Tsopano, ine ndikuwerenga kuchokera ku Ezekieli mutu wa 9, ngati inu mukufuna kuti muzilembe izo. Mvetserani mwatcheru:

> Ndipo. . . *Iye anafuula aponso mu makutu anga ndi liwu lokweza*, ndi *kunena, Apangitse iwo amene ali ndi ulamuliro pa mzindawo kuti ayandikire pafupi,. . . mwamuna aliyense ali ndi chida chawo chowononger a mu dzanja lake.* (Tsopano, uyu ndi Mulungu akuyankhula.)
>
> *Ndipo, taona, amuna sikisi anadza kuchokera ku njira ya chipata chakumbuyo, chomwe chiri* choloza *kumpoto, ndipo mwamuna aliyense chida* chophera *chiri mu dzanja lake; ndipo mwamuna mmodzi pakati pawo anavala bafuta woyera, ali ndi cholembera cha mlembi pa mbali pake: ndipo iwo analowa mkati, ndipo anakaima pa—pamphepete pa guwa lamkuwa.*
>
> *Ndipo ulemerero wa Mulungu wa Israeli unapita mmwamba kuchokera pa* akerubi, *pomwe Iye anali, mpaka ku chiundo cha nyumba. Ndipo iye anaitana kwa ine—kwa mwamuna wovala bafuta* woyera, ndi—anali ndi. . . cholembera mu dzanja lake—kapena pambali;

Ndipo chotero . . . Ndipo AMBUYE *. . .* (A-M-B-U-Y-E wa zilembo zazikulu, yemwe ali Mulungu.) *. . . Ambuye ananena kwa iye, Pita kudutsa mkati mwa mzindawo, kudutsa mkati mwa Yerusalemu, . . . ukaike chilemba pa mphumi ya munthu yemwe akuusa ndi . . . kulirira chifuka . . . cha zonyansa . . . zikuchitidwa mkati mwakemo.*

Ndipo kwa enawo iye . . . (AMBUYE) *. . . ananena ine ndiri kumva, Pitani inu momutsatira iye kudutsa mzindawu, ndi kukakantha: ndipo musalole diso lanu lilekerere, ngakhale inu musakhale ndi chisoni:* (Penyani, ndime ya 6.)

Kotheratu—Iphani kotheratu okalamba . . . aang'ono . . . adzakazi, . . . ana aang'ono, . . . akazi: . . . (Mulungu ananena chomwechoyo. Mulungu ananena chomwecho!) *. . . koma usabwere pafupi ndi munthu aliyense amene ali ndi chizindikiro; ndipo* iye *anayambira pa* wamakezana *. . . pa kachisiyo—ndi kuyambira pa munthu wamakezana . . . anali pamaso pa nyumbayo.*

180 Mwa kuyankhula kwina, Mulungu ananena kwa anthu awa, "Tsopano, dikirani; ine ndikuti ndikaike chizindikiro pa anthuwa choyamba, iwo amene ali odzipereka kwenikweni kwa Mulungu . . . " Ndipo Iye anaika chizindikiro pa iwo. Iye anati, "Tsopano," kwa amuna awa amene ali ndi zida zophera, "inu mupite modutsa ndipo inu musati mulekerere akazi, ana, kapena kanthu, koma muphe chirichonse psyiti."

181 Mu dziko lachigumula mu chiwonongeko, pamene mamilioni kuchulukitsa kamilioni ndi mabilioni a anthu anali pa dziko lapansi, ndipo Mulungu anatuma mlaliki wokalamba wachiyeretso kunja uko dzina lake Nowa, ndipo analalikira zaka handiredi n twente, ndipo anawauza iwo kuti abwere mkati mwa chingalawa, ndipo onse amene sanabwere mkati mwa chingalawa chimenecho akadati aonongedwe . . . Ndipo Mulungu wamphamvuzonse, yemwe anali ndi maulamuliro pa miyamba, anaitsitsira pansi mvula imene inaononga kotheratu mamilioni a anthu okalamba, a anthu achichepere, a makanda aang'ono, akupotedwa ndi kumaonongeka mmadzi.

182 Mulungu Wamphamvuzonse—ndipo Iye ali mokhozadi Mulungu wachikondi. Ndipo ndi zoona. Iye ayenera kutero. Iye amawakonda Ake omwe. Iye ayenera kukhala wochitamwayekha kwa Mawu Ake. Chotero osati kwa—mwa mtsutsano, koma kusagwirizana nanu. Mulungu wanu wa chikondiyo . . .

183 Kuno si kale litali ine ndinali kuyankhula . . . Anali kapena mwina wa Mboni za Yehova. Bambo anabwera apo ndipo anati,

"M'bale Branham, kodi inu mukutanthauza kuti mundiuze ine kuti inu mumakhulupirira kuli gehena woyaka?"

Ine ndinati, "Si chimene ine ndikunena, ndi chomwe Baibulo limanena."

Iye anati, "Inu mukutanthauza kuti mundiuze ine kuti Atate akumwamba wokondayo angadzawawotche ana Ake kotheratu? Chifukwa," anati, "inu simungamuwotche mwana wanu."

Ine ndinati, "Ayi, bwana!"

"Chabwino ndiye, ngati inu monga munthu muli ndi chikondi chochuluka chotero (mukuona, momwe anthu angakhoze kuchipindira chinthu mozungulira?)—ngati inu monga munthu muli nacho chikondi chochuluka chotero, inu mukuganiza kuti Atate akumwamba wokondayo angawaononge ana Ake?"

184 Ine ndinati, "Nzosatheka!" Iye samawaononga ana Ake, koma inu ndinu mwana wandani? Mulungu samawaononga ana Ake. Iye akuyesera mwakukhoza Kwake kuti awabweretse iwo mkati. Koma ndi mdierekezi yemwe wamasulidwa yemwe ati adzawaononge ana ake. Chotero Mulungu amangomuloleza Satana.

185 Penyani. Anali ndani amene analoleza choipa kuti chibwere pansi ndi Satana kuti apite kunja ndi kukaononga wantchito wangwiro kwambiri wa Mulungu mpaka Yesu Khristu, ana ake ndi chirichonse chomwe iye anali nacho—Yobu? Ndipo Mulungu anautuma mzimu woipa kunja uko ndipo anawaononga ana onse a Yobu ndi chirichonse kuti angomuyesa wantchito Wake. Ndi kulondola uko? Zedi.

186 O, ine ndikhoza kuima pano kwa ora ndi kumangokuonetsani inu izo, M'bale wanga, Mlongo. Uko nkulondola, yense yemwe inu mungakhale muli. Inu musati muutenge Mzimu uwu wa Mulungu mosokoneza. Nkhondo ndi ziweruzo za Mulungu pa mafuko. Zionongeko ndi zotumizidwa ndi Mulungu. Baibulo linanena chomwecho. Ndipo Mulungu ndi Mulungu wa chikondi, koma Mulungu ndi Mulungu wa mkwiyo naponso. Ndipo inu simuti mudzakaime pamaso pa wokonda . . . Icho chakhala chiri chinthu chimene chikuupweteka mpingo lero.

187 "Atate wina wokonda, ndithudi Iye sakanati asamale ine pomachita ichi." Ngati inu mukufuna kuti muzichite izo, inu mukanangoti basi mupitirire ndi kumazichita izo, chifukwa chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu pa kuyamba pomwe.

188 Ife tikukonzekera kuti tilandire Mgonero mu kamphindi chabe, ndipo ine ndikufuna ichi kuti chimire mwakuya kwenikweni. Chinthu chake ndicho, chimene chiri mu mtima mwanu chibala—nkupanga moyo wanu. Mtundu wa mbewu imene inu muika mu nthaka imadzabala mwa mtundu wake.

Inu mungatenge bwanji m—mmera wa chimanga cha mbuluuli ndi kupanga—udzu wa namgoneka kuchokera mwa iwo? Inu simungakhoze kuchita izo mopanda kuposa momwe inu mungakhoze kutengera njere ya chimanga ndi kupanga kanzota. Inu simungakhoze kuzipanga izo, chifukwa izo ndi zibadwa ziwiri zosiyana, miyoyo iwiri njosiyana palimodzi. I—i—inu mutati mutenge mbeu ya udzu wa namgoneka ndi mbewu ya anyezi, ndipo izo zimaoneka mofanana mwangwiro kwambiri mpaka munthu wodziwa kwambiri sangakhoze kuzidziwa izo molekanitsa. Ndiko kulondola. Chinthu chokha chomwe inu mumayenera kuti muchite ndicho kuzibzala izo. Izo zonse zimaoneka mofanana mwachilengedwe, koma zibzaleni izo. Izo zonse zidzabala; ndipo imodzi idzakhala udzu wa namgoneka ndipo inayo idzakhala ili anyezi. Ndiko kulondola ndendende.

189 Mukuti, "Chifukwa—nchiani chimaipangitsa mbewu iyi—iyo imaoneka ndendende basi monga iyi—nkumabala mtundu wa moyo wosiyana?" Ndi chifukwa mtundu wa moyo umenewo uli mkati mwakemo.

190 Ndipo mwamuna kapena mkazi amene angamadzinenere kuti ndi Mkhristu ndipo nkusamakhala moyo wa mtundu umenewo, mwa chisomo cha Mulungu, ali udzu wa namgoneka. Ndi zipatso zawo inu muziwadziwa iwo. Ngati chinthu chimenecho chiri mu mtima mwanu, chimachitira umboni za chimene inu muli kwinakwakenso. Ngati chiri choipa, icho chimachitira umboni chomwe inu muli pansi pano. Pamene inu mumwalira, inu mudzangoyenera kuti mupite kumene inu muli kaleko.

Ngati inu muli abwino ndipo inu muli—inu muli abwino chifukwa Mulungu wakupangani inu kukhala wabwino, ndipo inu muli obadwa kachiwiri, inu muli oti mupita njira imeneyo, chifukwa Moyo umenewo uyenera kuti uzichitirana umboni ndi malo awa. Ngati iwo ukuchitira umboni za kuno, uko ndi kumene inu mudzapita. Ngati iwo ukuchitira umboni kumwamba uko, uko ndi kumene inu mudzapita. Mwaona?

191 Chimene inu muli pano. . . Tengerani ichi mu malingaliro anu tsopano. Ine ndikuti nditseke. Koma chimene inu muli kuno ndicho chizindikiro kuti inu ndinu chinachake kwinakwake. Inu nthawizonse mwakhala mukufuna kuti mukhale mu ungwiro, inu Akhristu. Ulipo ungwiro, ndipo ungwiro umenewo suli mu moyo uno. Koma mwamuna aliyense ndi mkazi pano yemwe ali Mkhristu, munthu aliyense amene ali Mkhristu muno tsopano wapatsidwa kale ulemerero mu kukhalapo kwa Yesu Khristu. Ndipo inu muli nalo thupi lina. Inu simudzakhala nalo nthawi ina yake, inu muli nalo pakali pano. Pakali pano pali thupi lina likukuyembekezerani inu ngati ili liti lidzaonongeke. Kodi inu mungaganize za izo. Lingalirani izo miniti yokha.

192 Kodi inu mukudziwa kuti aliyense wa ife akhoza kukhala mu umuyaya dzuwa lisanatuluke mawa mmawa? Tsopano, ngati inu simuli Mkhristu, bwenzi langa, pali chinthu chimodzi chokha chatsalira kwa inu. Inu mukuyenera kuti mupite ku njira imeneyo. Ngati inu muli pa msewu umenewo, inu muyenera kuti mupite pa msewu umenewo. Ngati inu muli njere ya chimanga, inu muzibala chimanga. Ngati inu muli kanzota, inu muzibala moyo wa kanzota. Tsopano, ngati inu mwakhala muli wa ku mpingo kwinakwake umene sumadziwa ndipo sumaphunzitsa, ndipo amangokulolani inu kumabwera ku tchalitchi ndi kukhala membala wa mpingo. . . Inu mukuti, "Chabwino, M'bale Branham, mpingo wanga umaphunzitsa kuti ife tiyenera kumamulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wathu wathu. Ngati ife tikhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu ndife opulumutsidwa." Ngati moyo wanu suli kulingana ndi izo, ine simunafike pa izo panobe.

193 Kodi inu mukudziwa mdierekezi amakhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu? Kodi inu mumadziwa kuti Yesu pagulu—kodi inu mukudziwa mdierekezi pagulu anamvomereza Yesu kuti anali Mwana wa Mulungu? Ndipo iye sanali wopulumutsidwa. Ndipo iye sakanakhoza kupulumutsidwa; iye ndi mdierekezi. Chotero kumuvomereza Yesu kuti ndi Mwana wa Mulungu. . .

194 Kodi inu mukudziwa Afarisi onse aja ndi Asaduki, aliyense anali anthu odzifasitsa ndi achipembedzo kwambiri; momwe iwo ankamukondera Mulungu ndi mitima yawo, iwo ankaganiza; ndipo analephera kuti amuwone Mmodzi wosalakwa uja, Mwana wa Mulungu, kuti amuzindikire Iye kuti ndi Mwana wa Mulungu. Ndipobe, iwo anali achipembedzo kwambiri (nkulondola uko?), odzifasitsa kwambiri, ophunzira kwambiri, ankalidziwa Baibulo bwinopo kuposa aliyense wa ophunzira athu lero. Iwo analibe kanthu koti azichita koma kumakhala pamenepo kupyola mu mibadwo yawo ndi kumawatumikira Ambuye.

195 Tsopano, taonani chimene Lemba likunena: "Mu masiku otsiriza. . ." Kwa inu, abwenzi anga Achikhristu, ndi mwa chikondi chaumulungu, Baibulo linati, "Mu masiku otsiriza anthu—ikanadzafika nthawi pamene anthu akanati adzakhale ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zokondweretsa kuposa kukonda Mulungu." Tsopano, kodi izo si choonadi?

196 Munthu wina mu nyumba ino anapita ku phwando la Chaka Chatsopano usiku wina, ndipo mu chipinda chapansi iwo anali kulandira zakumwa zofewa ndi zosangalatsa ndi kumapitiriza, migonero ya ayesikirimu, ndi zina zotero. Mipingo imapereka ngakhale zovina. Kungokhala ndendende zimene Mulungu anawauza iwo kuti asamachite, iwo akuzichita mu Dzina la Khristu. Ndipo pano nachi chimene Yesu ananena kuti Mpingo uzichichita, ndipo iwo akuchikana icho. Yesu—

pano nawa Mawu Ake otsiriza, chifuniro Chake ndi pangano kwa Mpingo: "Pitani inu mu dziko lonse; kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene akhulupirira ndipo akabatizidwa adzapulumutsidwa; iye amene sakhulupirira adzalangidwa. (Mwina ndi mpaka apo pamene m'busa wanu anawerenga. Koma pano pali zonse zake.) Zizindikiro izi ziziwatsira iwo amene akhulupirira; mu Dzina Langa iwo azitulutsa ziwanda; iwo aziyankhula ndi malirime atsopano; ngati iwo atola njoka kapena kumwa zinthu zakupha, izo sizimawapweteka iwo; ndipo ngati iwo aika manja awo pa odwala, iwo azichila."

197 Tsopano, ndizo zomwe Yesu ananena kuti iwo azichita mu Dzina Lake. Iwo amakana kuti izo ziripo, koma iwo amapita ndi kumakachita basi mosiyana ndi chimene Iye ananena, kumaphunzitsa kuti izo nzakale, kulibe kanthu kwa izo, ndi kumaphunzitsa fioloje mmalo mwake. O, palibe zodabwitsa kuti ife tiri mu chikhalidwe chomwe ife tirimochi.

198 Tayang'anani kuno, ndiroleni ine ndikuuzeni inu, m'bale wanga. Pamene Mpingo ufika pa malo mpaka kuti . . . kuti membala aliyense mmenemo ali wopatsidwa nyetse ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu, mpaka zizindikiro izo zidzatsatira.

199 Ine ndikuganiza za Paulo Woyera kunja uko pa chisumbu pambuyo pa kuphwasuka kwa ngalawa. Mulungu anamupatsa iye masomphenya. Pamene masiku fortini ndi mausiku . . . Ziyembekezo zonse zitapita kuti iwo akanati apulumutsidwe. Bwato laling'ono, lakalelo kukukankhikira uku ndi uko monga choncho, ndipo iwo onse anali akulira, masiku fortini ndi mausiku. Paulo anali nawo uko, anali ndi masomphenya. Iye anatuluka kunja; ndipo iye anati, "Khalani olimbika bwino, pakuti Mngelo wa Mulungu, yemwe ine ndiri wantchito wake, anaimirira pambali panga ndipo anati, 'Usaope ayi, pakuti iwe uyenera kukabweretsedwa pamaso pa Kaisara. Ndipo taona, Mulungu wawapereka onse amene ali m'bwato ndi iwe.'"

200 Pamene ngalawa inaphwasuka ndipo anapita pa magombewo, ndipo iwo anafika cha uko ndi mbadwa, Paulo anali kutolera nkhuni zina, ndipo iye anapita nakaziika izo pa moto. Ndipo mmenemo munali njoka yaikulu, inamugwira iye pa dzanja. Tsopano, njoka imeneyo inabaira chiphe icho—mu dzanja lake chimene chikadati chimuphe iye mu miniti. Akumeneko anati, "Mumuone munthu ameneyo agwa nkufa, pakuti iye afa mu miniti yokha."

201 Iye ali mu unyolo chifukwa cholalikira Uthenga. Anthu achipembedzo anamuika iye mu unyolo. Mipingo yabwino kwambiri ya tsiku limenelo ndi imene inamuika iye mu maunyolo. Ngati likanati lisakhale Lamulo la United States, iwo akadadzachita chinthu chomwecho lero. Ndiko kulondola!

Ingodikirani mpaka iye ali—mpaka iye asweke moonjezekerapo pang'ono.

202 Ndipo njoka inamugwira iye cha pa dzanja. Tsopano penyani. Paulo sanaope ayi. Iye anati, "Yesu Khristu anati, 'Ngati iwo atola njoka, iyo siidzawapweteka iwo.'" Chotero iye anayenda mpaka apa, nkuikutumulira iyo pa moto; anatembenuka apo ndipo anayenda napita kukakatola nkhuni zina ndi kuziikanso pa moto; anadzitembenuza yekha ndi kuuwambitsa msana wake, ndi kutembenukira mbali iyi namauwambitsa manja ake. Akumeneko anati, "Bwanji iye sakufa? Chifukwa chiani munthu ameneyo sakufa? Iye amayenera kuti agwe nkufa." Koma Paulo anali wodzaza nawo kwambiri Mzimu Woyera (mukuona chimene ine ndikutanthauza?), wodzaza kwambiri ndi Mzimu Woyera mpaka chiphe icho sichikadamupweteka iye.

203 O, m'bale, ndipatseni ine mpingo wodzaza ndi Mzimu Woyera. Mulungu adzachita mu chaka chimodzi chimene afioloje onse analephera kuzichita mu zaka zikwi ziwiri. Inu mudikire mpaka kudzoza kwa Mpingo kugunde kwenikweni pachimake wotsalira wokhulupirika wapang'ono uja. Zitseko za Amitundu zikakhala zitatsekedwa, o, Mulungu adzaudzoza Mpingo apo. "Iye amene ali wonyansa, msiyeni iye akhale wonyansa apobe. Iye amene ali wolungama msiyeni iye akhale wolungama apobe, ndipo iye amene ali woyera msiyeni iye akhale woyera apobe." Ndipo Mulungu adzadzoza Mpingo ndi Mphamvu ya Mulungu, ndipo zinthu zidzakhala zikuchitika. Osati kokha apo ndiye, koma Iye akuzichita izo pano.

204 Penyani zizindikiro ndi zodabwitsa; ndiye anthu amayang'ana pozungulira ndi kumati, "Chabwino, izo ndi za mdierekezi." O, chifukwa iwo sakuwadziwa Malemba, ngakhale mphamvu ya Mulungu. Ndipo icho nchifukwa chake amanena izo.

205 Mulungu atakudalitsani inu. Ine ndikupepesa pokusungani inu mochedwa chonchi. Ine ndimachita izi mwakamodzi, koma ine sindimakhala ndi inu mochuluka kwambiri. Chotero ine mwina sindinawayankhe mafunso awa molingana ndi malingaliro anu ndi zinthu. Awo anali awiri amene anayankhidwa mmawa uno. Ngati ine sindinatero, Mulungu akudalitseni inu. Ndipo i—ine sindinatanthauze kuti—kukukwiitsani inu kapena chinachake. Ine ndimangoyenera kuti ndinene chimene . . . Inu mwandifunsa ine funso. Ine ndimachita zopambana za kudziwa kwanga kwa yankho. Ndiko kulondola.

206 Tsopano, ine sindikudziwa zochuluka kwambiri za zinthuzo mwina. Ine sindikudziwa chinthu chimene ine ndikuyenera kuti ndichidziwe. Koma chinthu chimodzi ine ndikudziwa, Yesu Khristu amatipulumutsa ife ku tchimo, amatitetezera ife ku tchimo, ndipo amatipatsa mphamvu Yake ndi madalitso Ake.

207 Ndipo ngati inu muti mungozindikira pozungulira ndi kuyang'ana chimene chikuchitika mwa anthu amene apemphereredwa . . . Tayang'anani kudutsa mu mafuko ndi kuyang'ana pa zizindikiro ndi zodabwitsa kulikonse. Ndipo tayang'anani pa nthawi ikubwerayo. Monga nthambi ziwiri zija ife tinazilalikira pano nthawi ina kalelo, zinadza kuchokera ku Genesis, momwe izo ziri kuchitira umboni kulikonse. Momwe osakhulupirira, achikhazikitso kwambiri ndi olemekezeka mu chipembedzo chawo, koma ali ndi maonekedwe aumulungu, koma nkumakana mphamvu yakeyo . . . Ndipo Mpingo uli kusunthira chitsogolo.

208 Ambuye Yesu atamudalitsa aliyense ndilo pemphero langa. Ndipo inu mutakhala moyo chotero kuti inu mukhale olemedwa kwambiri—mulole Mulungu aike pa anthu inu—kulemedwa kwambiri chifukwa cha miyoyo yotaika mpaka inu musamathe kugona usana kapena usiku. Mulungu atapereka kwa Branham Tabernacle uyu mwayi umenewo wa kukhala olemedwa kwambiri. Ine sindikusamala ngati inu simufuula konse, kapena inu simumachita kanthu kena kalikonse, ngati inu mutangokhala olemedwa kwambiri chifukwa cha miyoyo yotaika mpaka inu osamakhoza kugona. Pamene inu muti muchite izo, dziko likhala likumalowa muno kuti lidzapemphereredwe (ndiko kulondola!), dziko lidzabwera kuti lidzapemphereredwe. Inu mudzadziwika kulikonse. Mulungu atipatse ife za Mzimu Wake, atipangitse ife kudzichepetsa, atiphwasulire ife pansi, ndi kutipangitsa ife kukhala opatsidwa nyetse kwambiri ndi mphamvu ya Mulungu kuti tizichiritsa odwala, kuti tizitulutsira kunja ziwanda, kuti tizichita zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa. Pamene inu muziika manja anu pa odwala ndi kufunsa dalitso limenelo popanda kugwedera kumodzi mu mtima mwanu, inu nkumakhulupirira kuti Mulungu achichita icho. Penyani wodwala ameneyo, iye aziyamba kumakhala bwino moposerapo. Chifukwa? Choipacho chachoka kwa ife. Basi monga mtengo umene unali chiliri, Yesu anauyang'ana, ndipo umo munalibe chipatso mwa iwo. Iye anati, "Wotembereredwa ukhale iwe."

Maora twente-foro kenako iwo anadzadutsa pamenepo. Petro anati, "Taonani, masamba afota kale." Chinachake chinali chitachitika. Mawu a Mulungu anali atayankhulidwa.

209 Yesu anati, "Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Pakuti ngati inu munena kwa phiri ili kuti lisunthidwe, ndi kusakaika izo, ilo lizikumverani inu." Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu.

Tsopano, ino ndi nthawi ya Mgonero. Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu ine ndikuti ndimufunse winawake kuti abwere ku limba.

210 Ambuye, lino ndi oralo, nthawi yomwe mwina amuna ndi akazi, Ambuye, mu dziko lonse awona kuti ora lalikulu la chiweruzo liri kuyandikira pamene Mulungu adzaweruza mafuko onse mu maimidwe awo andale. Kulikonse, malo aliwonse, ndipo wina aliyense ayenera kuima nazo ziweruzo za Mulungu. Ndipo Atate, ife tiri okondwa kwambiri podziwa kuti palipo pothawira pa anthu awa amene—amene akadakhumba kuti athawe. Ndipo njira imeneyo ili kudzera mwa Yesu Khristu, amene ali m—Mphukira ya Davide. Ndipo ife tikukuthokozani Inu, Atate wokondedwa, pa kumutumiza konse Iye ku dziko lapansi, kuti Iye anali Mkhalapakati amene ife tikanati tizipitako; Inu mukanati muzititetezera ife, ndi kutichotsera machimo athu, kuti ife tikanati tithawe mkwiyo ndi chilango cha Mulungu. Ife tikudziwa kuti mkwiyo ndi woti ukudza. Ndipo kuti, monga Yohane ananena mu masiku apitawo, "Thawani ku mkwiyo umene ukuti ubwerewo."

211 Tsopano, Ambuye, ife tikupemphera kuti pamene ife tizitenga Mgonero usikuuno kuti Inu mutiyeretse ife, Ambuye, ndi Mwazi Wanu wotsukira; ndipo mulole tchimo lirilonse la anthu awa likhale litachotsedwa. Ine modzichepetsa ndi modzipereka ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu musalole mmodzi wa ife awutenge iwo mosayenera. Pakuti Inu mwanena mu Mawu Anu, ngati ife tichita chotero, ndife ochimwira Thupi ndi Magazi a Ambuye. Tsopano, Atate, apangitseni anthu awa kukhala oyera ndi odzipereka, kuti ife tikhoze kumatenga izi mopanda chilema.

212 Ndipo tsopano, Atate, ife tikuzindikira kuti Mgonero unayamba kuperekedwa kuja ku Igupto. Ndipo anthu awo amene anatenga Mgonero, mwanawankhosa ndi mkate, pamene iwo anali kuguba akutuluka, zaka makumi anai iwo anayenda ulendo mu chipululu; ndipo panalibe mmodzi wofooka pakati pawo pamene iwo anatuluka kuchokera mchipululu. Iwo anadya Mgonero.

213 Mulungu khalani wachifundo. Ine ndikupemphera kuti odwala onse achiritsidwe, otaika onse apulumutsidwe. Ndipo iwo amene ali ofunda ndi osayanjanitsika, mulole asendeze moyandikira ku moto wa Mulungu, kufunditsa miyoyo yawo. Perekani izo, Ambuye. Tikhululukireni ife tsopano ndipo mutithandize ife. Ife tikupemphera mu Dzina la Mwana Wanu.

214 Ndipo ife tikadali ndi mitu yathu yoweramitsidwa. Ine ndikudabwa (pamene m'bale azitipatsa ife kaimbidwe kakang'ono pa limba) ngati pali anthu pano amene akanakweza dzanja lawo ndi kuti, "M'bale Bill, ine—ine modzipereka . . . chifukwa cha khalidwe la moyo. I—i—ine ndikufuna inu mundikumbukire ine. I—i—ine ndikufuna kuti ndiulandire Mzimu Woyera." Inu mungakweze dzanja lanu? Muziti, "Mundikumbukire." Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu, inu, ndi inu. Mulungu

akudalitseni inu, ndi inu. Mulungu akudalitseni inu, Dona, inu, ndi inu, inu, M'bale. Mai, manja paliponse. Mulungu akudalitseni inu, M'bale. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, Mlongo. Inu, Mlongo, ine ndikuliona dzanja lanu. Kuti inu mukufuna kuti muulandire Mzimu Woyera. Mulungu akudalitseni inu, M'bale.

215 Kodi inu simukufuna kuyenda mongoyandikirapo pafupi pang'ono. Kumbukirani abwenzi, ife tiri kukhala mofupikira kudza kwa Ambuye wathu. Tsopano, Mulungu akutsimikizira Mawu Ake, zizindikiro ndi zodabwitsa kulikonse.

216 Tsopano, ndithudi Mulungu ameneyo sakanandirola ine kupita kunjako ndi kukakhala wodzozedwa ndi Mzimu Woyera kumakachita zizindikiro ndi zodabwitsa, nkubwera mmbuyo ndi kudzalalikira Mawu, ndi zina zotere, ndi kuzidalitsa izo kulikonse, ndi kumachita zinthu izi, kupatula Iye atandipatsa ine kumvetsa kwina kwa Mawu Ake. Iye sakanazipereka izo. Chotero ine ndikuchidziwa chimene ine ndikuchikamba.

217 Ndipo ngati inu muli opanda Yesu Khristu, opanda Mzimu Woyera, Mulungu asangokulekani inu kuti mukhale ndi mpumulo uliwonse mpaka inu mutalandira Mzimu Woyera. Musati mukhale onyengedwa. Musati mungotenga chimodzi cha zivomerezo zokhuthala za mmaso gwaa izi ndi kumanena kuti inu muli nao Mzimu Woyera. Inu simulandira Mzimu Woyera pamene inu mukhulupirira. Inu sikuti mumakhulupirira kuti mulandire Mzimu Woyera. Iyo ndi mphatso ya Mulungu. Paulo anati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuyambira pamene inu munakhulupirira?" Chotero khulupiririrani izo. Ndipo Mulungu ataupereka Iwo kwa inu.

218 Tsopano, Atate, kwa iwo amene anakweza manja awo mmwamba, ine ndikupemphera kuti Inu muwapatse iwo Umunthu wa Mzimu Woyera pakali pano. Iye atangobwera mozama mkati mwa ambiri awa—manja khumi kapena khumi ndi asanu amene anapita mmwamba. Ine ndikupemphera kuti Inu mupereke kwa mmodzi aliyense wa iwo ubatizo wa Umunthu Wanu. Mulole iwo akhale odzazidwa kwambiri ndi Mzimu Woyera, mpaka zizindikiro ndi zodabwitsa zizichitika mu miyoyo yawo, iwo aziona mitundu yonse ya zizindikiro. Monga Yesu anati, "Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira." Perekani izi, Atate. Ife modzichepetsa tikupemphera mu Dzina la Mwana Wanu, Yesu Khristu. Ameni.

Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo, Bukhu Loyamba
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org